

KUZINDIKIRITSIDWA

NDI KHRISTU

 Zikomo inu, mochuluka kwambiri. Ndine wokondwa kwambiri kubwereranso, mu Dzina la Ambuye. Wosasa mawu pang'ono chabe, kuyamba ndi kuyamba, koma Ambuye amandilola ine kuti ndilowe mu giyara yachiwiri, pakapita kanthawi. Chotero, ine ndakhala ndikuyankhula mochuluka sabata ino, pa msonkhano. Ndipo iwo akhala mafunso ambiri oti ayankhidwe. Ndiye nkutuluka mchipinda, mukutentha. Ndipo izo... Ine ndiribe chimfine choyipa. Ndipo ine sindinayambe ndamverera bwinoko konse, mmoyo wanga. Kotero, ine ndikungomverera bwino, koma kummero kwanga kwangotopa. Ndipo iko kukhala bwino. Chotero ine ndikufuna kuti ndithokoze mmodzi aliyense wa inu, chifukwa cha zonse zimene inu mwachita.

² Ine ndimayesetsa kuti ndipeze... Pamene ine ndimayendetsa, maminiti pang'ono apitawo, Billy ndi ena a iwo anali kunjako, kuyesetsa kuti apeze banja laling'ono limene labwera ndipo lashota, ndipo sangakhoze kubwerera. Ngati iwo akadali mchipinda muno, ine ndikukhumba ena... iwo akanakweza mmwamba dzanja lawo, kapena chinachake. Ine—ine ndimafuna chinachake pa zimenezo, inemwini. Ndipo chotero banja laling'ono lomwe liri lochokera ku Michigan, kapena kwinakwake, limene—limene mafuta awathera kapena chinachake, kapena ndalama. Ngati inu—ngati mukadali muno mu tauni... Ngati inu muwawone iwo msonkhano ukatha, muwadutsitsire iwo ku nyumba kwanga. Mukuona? Ine ndikufuna chinachake mu zimenezo. Ndicho—ndicho chimene—ndicho chimene ife tadzera pano, ndi kudzapereka dzanja lohandizira, aliyense amene ife tingathe. Chotero, tsopano, Ambuye Yesu tidalitseni ife, ndiro pemphero lathu.

³ Tsopano, ili lakhala sabata losazolowereka, ndipo ife takhala nazo zinthu zina zosazolowereka. Koma ine ndinena kuti ine sindinayambe ndawonapo nthawi imene Mzimu Woyera unayamba wasunthapo momasuka mulimonse kuposa momwe Iwo wachitira sabata ino, mu msonkhano, zakhala zodabwitsa mwangwiro basi kwa ine. Ndipo usiku pamene ine ndimalowa, nthawizina imakhala wani koloko mmawa ine ndisanapite kukagona. Ine ndimangosangalala mu malingaliro a Ambuye Yesu kukhala wabwino kwambiri kwa ife. Ndipo tsopano ine...

⁴ Aliyense wa anthu inu amene muli kozungulira kuno, mu mzinda, kapena oyandikana nawo, amene alibe nyumba

panobe, tchalitchi kwanu, ndinu olandiridwa kuno, kuti mubwere nthawi iliyonse ndi kudzapanga kuno kukhala kwanu. Kumbukirani, ife tiribe umembala kuno, chiyanjano basi cha onse. “Ife tiribe,” monga Howard Cadle ankakonda kunenera, “tiribe lamulo koma chikondi; tiribe kachikhulupiriro koma Khristu; tiribe bukhu koma Baibulo.” Ndipo chotero inu nthawizonse muli olandiridwa ku kachisi wamng’ono uyu.

Chimene, ife tikuyembekeza, ngati Ambuye alola, mwamsanga pamene ife tingathere, kuti tidzamange tchalitchi chabwinoko, kwambiri—malo ofunikira kwambiri. Osati chachikulu kwambiri, pakuti ife tikukhulupirira kuti Yesu akubwera posachedwapa, ndipo ife sitikufuna chinthu chapamwamba kwambiri. Ife tikungofuna chinachake... Ichi chiri pafupi kuti chigwere mkati. Icho chinatumikira cholinga chake, ndipo ndife othokoza kwambiri chifukwa cha icho.

Ine sindidzaiwala konse. Pomwepo pamene guwa ili layima tsopano, pafupifupi zaka twente chakuti zapitazo, ine ndinagwada mu dziwe lakale, mu udzu wa kavalo pa mutu wanga. Ndipo Ambuye anati, “Manga tchalitchi chako pano.” Pamalo aang’ono, amene ife tinapita kwa a Ingram ndipo tinakawagula iwo madolla handiredi ndi sikisite, ngati tikanadzawakwirira iwo. Ili linali dziwe la ayezi pamene ife tonse tinkadzalumphapo.

⁵ M’bale Jess Spencer ayenera kuti akukumbukira, ili linali dziwe muno, iye ndi Mlongo Spencer. Ine ndikuganiza inu mukukumbukira zimenezo. Iwo ankakonda kubweretsa ma timu, ndi kudzayendetsa mozungulira njira *iyi*, kupewa kuti asalowe mu dziwe.

Ine ndinali mnyamata wamng’ono kuno ku Sukulu ya Ingramville. Ili linali dziwe; kutuluka kuno ndi kuyenda pa ayezi, ndi—ndi kusewera mpira wa pa chipale ndi china chirichonsecho, pa dziwepo. M’bale Mike, inu mukukumbukira pamene ili linali dziwe. [M’bale Mike akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Inde, bwana. M’bale Roy, kumbuyo uko.

Ndipo tsopano, pamene dziwe linaima, ife tinangotenga gawo lake kumanzere, kumbuyo komwe *kuno*. Ndi pamene ife timawabatiza anthu mmadzi kuloza ku chikhululukiro cha tchimo lawo. Ndipo tsopano izi...

⁶ Inu mukudziwa, pamene inu mubweretsa mafunso kuno, ndi pamene inu—inu mukhala ndi chinachake chimene inu mukufuna kuti muchipereke, ndipo ndi vuto chifukwa iwe umakhala ndi omvetsera osakanizika. Anthu aphunzitsidwa mwanjira ina kapena imzake. Koma pamene iwe ungakhoze kuchifotokoza chinthucho, ngakhale mosiyana ndi momwe iwo anaphunzitsidwira, ndipo kukoma kwa mzimu wawo kumayenderera mmbuyo, ndicho chaumulungu, kwa ine.

Ine sindikufuna kuti ndibweretse dzina linalake lirlonse. Koma a—dokotala winawake, wochokera kunja kwa mzinda, anangokumana nane ine mchipinda mmenemo; dokotala wazamankhwala, ine ndikuganiza. Ndipo, iye anati, kwa zaka iye wakhala ngati wasokonezeka mu zimenezo. Iye anawerenga bukhu limene linalembedwa lokhudza zimenezo, motsutsana ndi zimene ine ndinali kuphunzitsa. Koma, anati, kuyambira pamene iye wakhala ali mu msonkhano, ndi kuwona zoonza za Lemba zikuikidwa, izo zakhazikitsa izo kwanthawizonse.

⁷ Kanthawi kapitako, ine ndimakomana mchipinda, ndi anthu ena ochokera kunja kwa mzinda, ochokera ku Illinois. Ndipo munalipafupifupi atumiki anayi, atumiki atatu kapena anayi. Ndipo iwo anati, “M’bale Branham, ife taphunzitsa zosiyanika, moyo wathu wonse, koma ife tagwira masomphenya tsopano ndi kuwona chimene kwenikweni chiri Choonadi. Ife takhala tikudabwa chimene icho chinali.” Mukuona? Ndipo tsopano, zimenezo, onani, izo ndi zimene ife tiri tsopano . . .

⁸ Basi chimene izo ziri, m’bale, musati muganize kuti izo zikuchepesya mpingo uliwonse kapena anthu aliwonse. Izo zimangowubweretsa Mpingo pamwamba. Mukuona? Ndiyenso, pamodzi, ife tiyenera kuima. Ife tiyenera kuima limodzi. Pamene iwo . . .

Pamene Mulungu anadzigawaniza Yekha pa Pentekoste, kugawa Lawi la Moto kukhala tating’ono, timalawi ting’onoting’ono ta Moto, ndipo anapita ndipo anakapachikika pa anthu, ndipo Mzimu Woyera unabwera pa iwo, ngati Mulungu anadzigawaniza Yekha pakati pathu, nthawi iliyonse imene mmodzi adziwonjezera yekha kwa ife, zimenezo zimawunjikana mochuluka pozungulira Lawi limenelo, nthawi zonse. Ndipo pamodzi, pamene ukhala Mpingo wonse wawukulu wowomboledwa wa Mulungu, ukokedwera pamodzi, ife tidzatenga ulendo kudutsa mu mlengalenga, motsimikiza basi monga chirichonse.

⁹ Ine sindinayambe ndayeserapo kuti ndilekanitse kapena kufesa kusagwirizana pakati pa abale. Ine ndayesetsa mwakukhoza kwanga kuti ndikhale monga momwe ine ndikanathera, kuti ndimvetse. Ndipo—ndipo amuna ena, ngati iwo . . . matchalitchi amene amathandizira msonkhano wanga. Ndiye ngati iwo ali . . . Iwo ali osiyana wina ndi mzake, koma iwo amandikonda ine, ndipo iwo amathandizira misonkhano yanga. Ndipo ine ndimabwera pakati pa anthu amenewo, ine ndithudi sindingati ndinene chinthu chimodzi. A—njonda singachite zimenezo, ngakhale Mkhristu. Ayi ndithudi.

Ndiyenso ngati ine ndidzakhale ndi misonkhano ya hema; imene ine ndikusinkhasinkha zodzachita, Ambuye akalola, tsiku lina. Ndiye ine—ine ndidzatero, ine ndisanaphunzitse chirichonse cha zophunzitsa izi, poyamba kudzakhala

misonkhano ya mmawa ndi azibusa, kwa masiku angapo, kudzawadziwitsa iwo chimene ine ndikukonzekera kuti ndiphunzitse. Ndiyen ngati m'bale ameneyo sakuziwona izo ndipo sakugwirizana nazo, m'bale aliyense, ndiye iwo alitenge gulu lawolo, ndikuti, "Tsopano, ine sindikufuna kuti inu mumvetsere izi. Ife tingokhala kutali pamene iwo aziphunzitsa Izo." Mukuona? Ndi kuwapatsa iwo mwayi. Ife nthawizonse timafuna kukhala mu chiyanjano ndi Mulungu ndi ana Ake, ndi aliyense.

¹⁰ Chotero, tsopano, ine ndiri ndi funso loti ndiyankhe usikuuno, Ambuye akalola. Ndipo ine ndinaganiza mwinamwake ine ndingoyankha funso ili, basi ndisanati. Ine ndimaganiza kuti ndinali ndi lina apa, koma ilo linali loto limene winawake anali atapereka, ndipo amafuna kuti ine ndizipempherere izo ndi kupereka kutanthauzirako. Chimene, Ambuye akhala achisomo kwambiri kwa ife, kuti tizichita zimenezo, nthawi zochuluka kwambiri.

¹¹ Tsopano, ife tikufuna kuti inu mudziwe, ife tisanayambe mu msonkhano, kuti ndinu nonse oitanidwa movomerezeka kubwerera ku msonkhano uliwonse, nthawi iliyonse imene ife tikukhala nawo wina. Ndipo kuchokera ku Louisville, kuchokera kunja kwa mzinda, kuchokera mu mzinda ndi kozungulira pafupi; atumiki abwino awa; m'bale wochokera ku Sellersburg; oyimba; dona uja, yense yemwe iye anali, amaimba kunja kuno, kanthawi kapitako, ndi mnyamata wamng'onoyo. Ife tikungokuthokozani inu, mochuluka kwambiri. Ine—ine ndinali kuyankhula ndi abale ena kumbuyo uko, ndipo ine sindinapeze nkomwe mwayi woti ndimuwone yemwe iye anali, ndipo chimene icho chinali, koma ine ndithudi ndinachimva icho. Ndipo icho chinali chokongola, ndipo ine ndithudi ndikuyamikira kuyesetsa kumeneko. Tsopano ife ti . . .

¹² Ine ndinaphonya ichi usiku wathawu. Mwana wanga anachiyika icho mu thumba langa. Munthu wina wofunika analemba icho. Ndipo tsopano kumbukirani, mafunso awa si akuti tikhale osemphana. Nthawizina, mwinamwake, pamene iwo alembedwa, iwo amamveka ngati iwo ndi otsutsa, koma ndi mtima woona ukuyesetsa kuti ufufuze. Mukuona? Umo ndi momwe ife nthawizonse timafikira pa zimenezo, munthu woonamtima winawake weniweni akuyesera kuti apeze chomwe chiri cholondola.

¹³ Tsopano, kuno nthawi ina kale, ine ndinapita uko kunyumba, ndinali ndi msonkhano wa pemphero. Ndipo M'bale Junior Jackson, ine ndinamumva iye kanthawi kapitako, kapena ine ndimaganiza kuti ndinatero, iye anali ndi ine. Ndipo iye anali atatsiriza kuyankhula. Ndipo apo panali mtumiki wochokera ku mpingo wina. Ndipo ine ndisanafike konse pansi, iye analumpha mmwamba ndipo anayamba, ankafuna kuti akangane ndi ine. Chabwino, panali pafupifupi

atumiki faivi kumeneko, ndipo iwo onse anali oti akwere pa mwamunayo nthawi imodzi. Ine ndinati, “Ayi. Musachite zimenezo. Tsopano, iye—iye wandibetchera ine, chotero mulole iye ndi ine tikambirane zimenezo.”

Chabwino, iye anayambapo, “Ife timayankhula pamene Baibulo likuyankhula; chete pamene Ilo liri chete,” ndi zina zotero. Ndipo iwo anachokapo. Ndipo basi mu mphindi pang’ono... Ine ndinapitirira kumalemba Malemba amene iye anali akubwereza molakwika, kuwaika polakwika. Anati, “Panalibe koma—pamenepo panalibe koma anthu thwelovu anayamba alandirapo Mzimu Woyera. Amenewo anali atumwi. Ndipo machiritso Auzimu anangoperekedwa kwa thwelovu amenewo,” ndi zina zotero. Chotero, inu mukuona, iye anangophonya chandamale, ndi mamailosi milioni. Chotero patapita... ine... Patapita pafupifupi theka la ora la iye akuyankhula, ine ndinamufunsa iye... Ndipo iye anati ine ndinali mdierekezi.

¹⁴ Ndipo kotero ndiye, atamaliza kuyankhula, ine ndinati, “Tsopano, chinthu choyambirira chimene ine ndikufuna kuti ndinene, m’bale, ine ndakukhululukira iwe chifukwa cha zimenezo, chifukwa iwe sumatanthauza zimenezo. Ine ndikudziwa iwe sunatero. Pakuti, ngati ndiwe mtumiki ndipo ndine mtumiki, ife tiyenera kukhala abale.” Mukuona? Ndiyeno ine ndinati, “Tsopano, kusamvetsetsana wina ndi mzake, mu Lemba, ndi chinachake chosiyana.”

¹⁵ Kotero ndiye ife tinayamba kutenga Lemba. Ndipo munthu wosaukayo anataika kwambiri, mu miniti, iye sanadziwe kuti ayime pati kapena choti achite. Kenako, iye anamangiridwa kwambiri, iye sanadziwe choti achite. Ndipo iye, pamene iye amatuluka mchipindamo, ngakhale, usiku umenewo, iye anati, “Ine ndinena chinthu chimodzi, M’bale Branham. Inu muli ndi Mzimu wa Khristu.” Mukuona?

Ndipo ine ndinaganiza, “‘Mdierekezi,’ maminiti pang’ono apitawo, ndipo tsopano ‘Mzimu wa Khristu.’” Ndi basi momwe umazifikira izo. Ndizo zonse. Khristu sanali woti azikangana.

¹⁶ Tsopano—tsopano, munthuyo, chifukwa chakuti iye anachita zimenezo, zinthu zowopsya zinamuchitikira iye; pafupifupi kusokonezeka mmalingaliro ake. Kuchokera kosunga amisala kapena chinachake, analumphira pa zenera, ndipo anatsala pafupifupi kuti adziphe yekha. Ndipo tsopano iye akubwerera kwa abwenzi ena abwino a ine. Iye akufunafuna, tsiku lirilonse, ubatizo wa Mzimu Woyera. Akufuna kuti abwere ku nyumba yanga, kuti adzasanjikidwe pa iye, kuti alandire Mzimu Woyera; mlaliki wa chipembedzo chachikulu cha mpingo. Mukuona?

¹⁷ Kotero, moona mtima ife timayankha mafunso, ndi zonse zomwe ife timadziwa momwe tingayankhire.

¹⁸ Ndipo tsopano ine ndiwerenga funso ili, lolembedwa bwino.

1. M'bale Branham, kodi inu chonde mungafotokoze chifukwa chimene anthu mu Machitidwe 2:4 anayankhulira mmalirime ena kapena zinenero, ngakhale unyinjira usanabwere pamodzi mu Machitidwe 2:6?

Limenelo ndi funso loyamba. Eya. Ndi munthu yemweyo, ine ndikuganiza, aponso. Inde, ndi munthu yemweyo.

¹⁹ Chabwino, tsopano, ngati inu mungazindikire, m'bale, mlongo, yense yemwe iye anali yemwe analemba ilo. Ilo silinanene konse mawu akuti amatsikira zipinda zapansi, kuchokera pamwamba. Ndipo omvetsera sanali pamwamba. Koma pamene iwo anadzatsikira ku mabwalo kumene khamulo linasonkhana, ndi pamene iwo anawamva iwo akuyankhula mmalirime. Mukuona? Mukuona?

²⁰ Tsopano, inu mukhoza kunena kuti, "Chabwino, iwo anayankhula pamwamba apo."

Ndipo ngati unali mtsutsano kapena mkangano, inu mukanakhala ndi ufulu wochuluka basi wonena kuti, "Iwo sanayankhule kufikira atafika pansi apa, chifukwa, 'Pamene izi zinamveka kunjako.'" Mukuona?

Tsopano, chinthu china apa, icho chikuyenda limodzi ndi ichi.

2. Kodi mungafotokoze momwe Simoni ankadziwira kuti Mzimu Woyera unali utaperekedwa mu Machitidwe 8:18? Uko ndi ku Samaria.

²¹ Chabwino, pali chinthu chimodzi, iye sanadziwe kuti iwo anali ndi Mzimu Woyera chifukwa cha kuyankhula mmalirime, kapena Baibulo silinanene kuti iwo anatero. Iwo anangowona zotsatira. Palibe amene angalandire Mzimu Woyera popanda kukhala ndi chinachake chikuchitika kwa iwo. Uko nkulondola. Koma ilo silinanene kuti iwo anayankhula mmalirime kumeneko, chotero icho chiyenera kuti chinali chinachake chimene iye anachiwona pambali pa kuyankhula mu lirime, chifukwa ilo silinatchule konse kuti iwo anayankhula mu lirime.

3. Ndipo tafotokozani momwe ife timadziwira kuti ena a anthu pa Tsiku la Pentekoste anayankhula chi Galileya.

²² Gawo lalikulu kwambiri la iwo linali Agalileya. Ndipo onse a iwo . . . Tsopano, monga ine ndinanena mmawa uja . . . Tsopano, pali zinthu ziwiri, mphamvu ziwiri. Tsopano, ine nditenga mbali imene anthu anali kuyankhula mmalirime; anthuwo ankayankhula osati mmalirime, koma mu zinenero, pamene iwo anatuluka mu chipinda chapamwamba ndipo anayamba kukumana ndi anthuwo. Koma ngati inu mungawerenge Lemba, mveterani mwatcheru tsopano.

. . . *kodi awa onse si Agalileya amene akuyankhulawa?*

Ndipo bwanji ife tikumva—bwanji ife tikumva munthu aliyense mu lirime lathu lomwe, mmene ife tinabadwira?

...kodi awa onse si Agalileya amene akuyankhulawa?

²³ Iwo akhoza kukhala kuti ankayankhula Chigalilea, koma amawamva iwo mu chinenero china. Izo zikhoza kukhala kuti iwo anali akuyankhula chinenero china, chinenero chawo chomwe. Mulimonsemo, zinalibe kanthu; izo sizikupangabe lingaliro la Chipentekoste kukhala lolondola. Mukuona? Chifukwa...Mvetserani. Chifukwa chake ndi ichi. Osati kuti ndinene chinachake chosiyana, koma kungoti ndipange choona molunjika. Ngati mungazindikire, nchifukwa chiyani Petro anamirira pamenepo ndipo nkudzayankhula kwa gulu lonselo, ndipo iwo mmodzi aliyense anamumva iye mu chinenero chimene iye anali kuyankhula. Pakuti, firii sauzande anatembenuzidwa, a Ayuda okhazikika amene anali okhazikika mu chipembedzo chawo monga iwo akanakhoza kukhalira. Koma iwo ayenera kuti anaima, anamvetsa mawu aliwonse, a Petro akulalikira pa aneneri, ndi zina zotero, akubweretsa ku Pentekoste. Pakuti iwo anafuula mokweza, ndipo anati, “Amuna ndi abale, kodi tichite chiyani kuti tipulumutsidwe?”

Petro anati, “Lapani, ndipo mubatizidwe mmodzi aliyense wa inu mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha tchimo lanu.”

²⁴ Tsopano mungondilola ine ndinene izi, ndi—ndi...mtima wanga wonse, kuti inu muwone...chimene ine ndikuyesera kuti ndichifikitse kwa inu. Ine ndithudi ndimakhulupirira mu kuyankhula mu lirime. Ine ndimakhulupirira kuti iyo ndi mphatso kwa Mpingo. Ine ndimakhulupirira kuti pali lirime. Ine ndayankhulapo mmalirime, nthawi zambiri, inemwini.

²⁵ Ndiroleni ine ndikupatseni inu chitsanzo chaching’ono, chimene ine ndikuganiza kuti Pentekoste inali. Ndiyeno ine ndidza...chinachake chonga chimenecho, tsopano, kapena chinachake mwa dongosolo ili. Ine ndinali ku Dallas, Tex-... Houston, Texas, basi chithunzi *ichi* chisanajambulidwe, pafupifupi tsiku lina. Ife tikanakhoza kutenga Music Hall; ife tinali ndi eyiti sauzande. Anthu sakanakhoza kulowa mmenemo, kotero ife tinapita ku kachisi wa Raymond Richey. Ine ndaiwala basi...Uyo anali wamkulu, kachisi wamkulu. Ndipo—ndipo ife tinadzaza mmenemo. Ndipo ine ndimakhocha kulalikira ndi kupempherera odwala, kumeneku. Ndiye, pamene iwo akuwatulutsa iwo panja, ine ndinkapita kumeneko, ndi kukalalikira ndi kuwapempherera iwo cha kuno, kwa Raymond Richey, kuwoloka mtsinje.

²⁶ Ndiyeno pamene ife tinali kumeneko, tikukonzekera kuti tibwerere ku Music Hall, ine...Howard anali atangondilola ine kuti ndipite kutali momwe ine ndikanathera. Ndipo iye

anandikhudza ine pa phewa, anandisisita ine pambali. [M'bale Branham akuzisisita pa iyemwini—Mkonzi].

Ngati inu munazindikirapo, mchipinda, pamene kudzoza kukuchitika, iwo amandisisita ine, monga *chonchi*. [M'bale Branham akuzisisita yekha—Mkonzi]. Izi zimatanthauza kuti, “Ndi nthawi yoti musiyey. Musayankhulenso zina. Chokanipo.” Ndipo Howard, ankakonda kukhala, ine ndimakhoza kuima pamenepo, iye amakhoza kungotenga dzanja langa, kundiponyera ine pa phewa lake ndi kumayenda akutuluka. Mukuona? Chifukwa, iye ankadziwa kuti ndinali nditapanga zokwanira.

Chabwino, ine ndinayamba kuchoka pa nsanja pamene iye anandisisita ine. Ine ndinati, “Chabwino, m'bale.” Ndinayamba kuchoka pa nsanja, ndipo mtsikana, mtsikana wamng'ono, anali atakhala, ataimirira apa, akulira. Mtsikana wamng'ono, wa chi Mexico, ankawoneka kuti anali pafupifupi usinkhu wa zaka thwelovu, fortini, usinkhu wa mmadini basi. Ndipo ine ndinayang'ana pa iye, ndipo ine ndinati, “Chavuta ndi chiyani, wokondedwa?” Ine ndinati, “Iye akulira, Howard, chifukwa . . .”

Anati, “Iwe wachita zokwanira. Iwe uli ndi gulu lina uko, likudikirira.”

Ndipo ine ndinati, “Mbweretseni iye kuno.” Ndipo ine ndinangofikira pamenepo, ndinamukodola monga *choncho*. Ndipo iye anadzabwera pa nsanja. Ine ndikukhulupirira M'bale Wood ndi iwo analipo, tsopano. Iwo analipo pa msonkhanowo. Ine sindikudziwa kaya pa nthawi imeneyo kapena ayi. M'bale Wood, kodi inu muli pati, usikuuno? [M'bale Banks Woods akuti, “Pano.”—Mkonzi]. Anali . . . Nkulondola uko? [“Kulondola.”] Eya, inu munalipamenepo. Ndipo ine ndinati, “Mbweretseni iye pa nsanja.”

Chabwino, ine ndinati, “Taona, wokondedwa. Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu ndi wokhoza kundiuza ine lomwe liri vuto lako?” Ndipo iye anangoweramitsa mutu wake waung'ono pansi. “Chabwino,” ine ndinaganiza, “iye akhoza kukhala wosamva ndi wosayankhula.”

²⁷ Chotero, ine ndinayang'ana kachiwiri. Ine ndinawona kuti izo zinali kuyankhula. Ndipo ine ndinati, “Oh, iye sangakhoze kuyankhula Chingerezi.” Iye samatha kuyankhula mawu amodzi a Chingerezi. Chotero iye anali wochokera ku Mexico. Chotero iwo anali ndi wotanthauzira kuti abwere. Ndipo ine ndinati, “Kodi inu mukukhulupirira, wokondedwa, kuti Ambuye Yesu akhoza kundiuza ine lomwe liri vuto lanu?”

Chabwino, iye anayankhula moyankha wotanthauzira, anati, “Inde. Iye anakhulupirira izo.”

Ndipo ine ndinati, “Kodi inu simungakhoze kuyankhula Chingerezi, nkomwe?” Ndipo wotanthauzirayo ananena kwa iye.

Iye anati, “Ayi.” Iye sankadziwa konse mawu aliwonse a Chingerezi. Iye anali wochokera ku Mexico. Ndipo chotero pamene ine . . .

²⁸ Ndiye masomphenya anayamba. Ndipo ine ndinati . . . Iwo satanthauzira masomphenya, mwaona, chifukwa iwe umayankhula mosalekeza. Samanthauzira konse masomphenya, kotero, mpaka izo zonse zitatha, ndiyeno iwo amawauza iwo zomwe zinachitika. Chotero, ndiye, pamene ine ndinayamba kuyankhula, ine ndinawona masomphenya. Ine ndinati, “Ine ndikumuwona mtsikana wamng’ono wa pafupifupi usinkhu wa zaka sikisi. Iye wavala diresi ya mandalasi, yomwe ili ndi mizere yakuda ikulendewera kumbuyo kwake, ndi mauta a riboni mmenemo. Iye wakhala pafupi ndi malo a moto achikale. Pali ketulo yaikulu, ndipo iye akudya chimanga chachikasu kuchokera mwa iyo. Iye amadya chimanga chochuluka mpaka iye amadwala mwachisawawa. Iye amagwa, ndipo amayi ake amamugoneka iye pa bedi, ndipo iye amakhala ndi khunyu. Ndipo ndicho chimene chinachitika kwa iye. Mukuona?” Ine ndinati, “Iwe unali ndi khunyu, kuyambira pamenepo.”

Ndipo mwamsanga, aliyense asananene kalikonse, iye anayang’ana mmwamba kwa wotanthauzira, iye anati, mu chinenero chake chomwe, “Ine ndimaganiza kuti iye samatha kuyankhula chi Spanish.”

Ndipo wotanthauzira anati, “Kodi inu mumayankhula chi Spanish?”

Ine ndinati, “Ayi, bwana. Ine ndinayankhula Chingerezi.”

Iye anati, “Chabwino, iye anati inu munayankhula Chispanishi.”

Ine ndinachigwira icho. Ine ndinati, “Imitsani zojambulirazo.” Pamenepo panali gulu lalikulu la zojambulira, mwinamwake sarte za iwo zikuyenda, masiku amenewo.

M’bale Roy Roberson, kodi inu simunali kumeneko? [M’bale Roy Roberson akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Inde. M’bale Roy Roberson, ndi Mlongo Roberson ndi iwo, anali pamenepo.

²⁹ Kotero ine ndinati, “Imitsani marekodawo. Sewerandinso iwo.” Ndipo izo zinali kwenikweni mu Chingerezi. Koma, inu mukuona, ndiye pamene ine ndimayamba . . .

Utali wonse masomphenyawo anali akupitirira, ine ndinali kuyankhula Chingerezi koma iye anali akuzimva izo mu chi Spanishi. “Ife tikumumva bwanji munthu aliyense mu lirime lathu lomwe, mmene ife tinabadwira?” Mukuona? Ndipo, koma, mwamsanga pamene ine ndinayamba kuyankhula, inemwini, ndiye iye sanamve chinthu chimene ine ndimanena. Koma pamene kudzoza kunali pa . . .

³⁰ Tsopano muziyike zimenezo ku Pentekoste, kamodzi kokha. Mukuona? Mzanga, Mulungu ndi wondiweruza wanga. Mzimu

Woyera unachita zimenezo. Tsopano tiyeni tiziyeke izo mmbuyo ku Pentekoste, kwa tanthauzo lathu. Mzimu Woyera sungachite chirichonse basi—basi kuti ndinene kuti Iye anachita zimenezo. Ichochiyenera kukhala choyambitsa ndi chifukwa. Mukuona?

³¹ Tsopano, pa Tsiku, “Bwanji ife tikumumva munthu aliyense mu lirime lathu lomwe, kumene ife tinabadwirako? Kodi onsewa siali, akuyankhulawa, Agalileya?” Kodi iwo anadziwa bwanji kuti iwo anali Agalileya, ngati iwo sanali kuyankhula chi Galileya? Iwo onse amavala mofanana. Iwo anadziwa bwanji kuti iwo anali Agalileya? “Kodi onsewa siali, amene akuyankhulawa, Agalileya? Ndipo bwanji ife tikumumva munthu aliyense, mu lirime lathu lomwe, kumene ife tinabadwirako?”

³² Ndiye, pamenepo panadzuka mwamuna wina, wa chi Galileya, Petro, ndipo anayamba kulalikira kwa iwo. Ndipo mwanjira ina imzake, mu unyinjira uwo wa anthu, miyoyo firii sauzande inamumvetsa iye, ndipo inabwera ndipo inadzatembenezidwa, ndipo inapereka miyoyo yawo kwa Khristu.

³³ Tsopano mvetserani. Ndiroleni ine ndingokutengerani inu Lemba limodzi lina, chonde. Tiyeni tipite kwa Paulo Woyera wamkulu, ndiyeno ife tiwerenga mutu wa 12 wa Akorinto Woyamba. Ndiyenso tigwere mu mutu wa 13 wa Akorinto Woyamba, pamene Paulo akuyankhula za, “Ngati makutu anganene kwa mphuno, ‘Ine sindikukusowa iwe,’” ndi zina zotero, mamembala a Thupi. Ndiye mu mutu wa 13—mutu wa 13, mvetserani zimene iye ananena tsopano.

³⁴ Tsopano, ife tikudziwa kuti pali mitundu iwiri yosiyanasiyana ya malirime imatchulidwa mu Baibulo. Amodzi a iwo ndi chinenero, kuti ndi—ndi chinenero cha padziko lapansi. Tsopano, chinacho ndi lirime losadziwika.

³⁵ Tsopano, ambiri a anthu anga ofunika kwambiri... Ine ndakuuzani inu kuti ndine wa Pentekoste. Tsopano, ambiri a anthu anga amakhulupirira zimenezo, kuti, pamene iwo alandira Mzimu Woyera, iwo amangoimirira ndi kuyankhula mu lirime losadziwika. Ndizo ndendende zotsutsana ndi Lemba. Ndiye anthu samadziwa chimene iwo akunena. Koma, pa Tsiku la Pentekoste, aliyense ankadziwa chimene iwo anali kunena. Uko kunali kupita, ku fuko lirilonse. Mukuona? Yesu anati, “Uthenga uyenera kulalikidwa kwa dziko lonse, kuyambira ku Yerusalemu.” Apo ndi pamene izo zinkayenera kukhala mwanjira imeneyo.

Tsopano zindikirani. Paulo ananena, kuti, “Lirime limodzi, kuti, ngati mutayankhula mwa ilo, lirime losadziwika lomwe liri mphatso ya malirime, kupatula izo zitakhala mwa kutanthauzira kapena mwa vumbulutso, kuti izo sizingapindulire mochuluka.”

Ndiyeno ife tikupeza, kuti, mu mutu wa 13, iye anati, “Ngakhale ine ndingamayankhule ndi malirime a anthu,” ndicho chiyanikhulo cha dziko lapansi, “kapena a Angelo. Ngakhale ine ndingayankhule ndi lirime la anthu kapena la Angelo, ndipo ndiribe chikondi, sindine kanthu.” Chotero iwe ukhoza kuyankhula ndi malirime enieni awiri onse a anthu ndi Angelo, ndipo komabe iwe ulibe Mzimu Woyera.

³⁶ Kodi ife sitinangokhala nazo zimenezo, mu Ahebri 6? “Mvula inagwera pa tirigu ndi maudzu.” Kodi Yesu sanati, “Mvula imabwera pa olungama ndi osalungama”? Mukuona? Mvula yomweyo imene imapangitsa tirigu kukula, ndi mvula yomweyo imene imapangitsa a—a...kukula. Koma, ndi chipatso cha zimenezo, inu mukudziwa izo.

Ndipo chipatso choyambirira cha Mzimu ndi chikondi. Chimene Paulo ananena, “Ngati ine nditakhala—ngati nditakhala nazo zonse, kukhoza kuyankhula mu mitundu yonse ya malirime, ndipo ndiribe chikondi, kuleza mtima, chifundo, chikhulupiriro, chipiriro, ndi zina zotero, izo sizindipindulira ine kanthu.” Mukuona?

³⁷ Ndiyeno zindikirani za mphatso. Inu mukuti, “Oh, *pali* munthu wamkulu wa Mulungu. Oh, iye amachita zozizwitsa.” Izo apabe sizimamupangitsa iye kukhala wolondola.

³⁸ “Ngakhale ndingakhale ndi mphatso ya zozizwitsa,” Paulo anatero, mu Akorinto Woyamba, chinachake mwa dongosolo limenelo, “ngakhale nditakhala ndi chikhulupiriro mpaka ine ndikhoza kusuntha mapiri, ndipo osakhala ndi zipatso za Mzimu, chikondi, ine sindiri kanthube.” Mukuona? Chifukwa, chikhulupiriro chimachita chirichonse.

Ndi chifukwa chake ine nthawizonse ndimati, “Inu simumachiritsidwa ndi kuyenera kwa chipulumutso chanu. Kuyenera kwanu...kuchiritsidwa ndi kuyenera kwa chikhulupiriro chanu, ‘Ngati inu mungakhulupirire.’”

³⁹ Tsopano, onani, “Ngakhale ndingayankhule ndi malirime a anthu ndi Angelo, ndipo nkusakhala ndi chi-...,” ngakhale iye akanakhoza kuchita zimenezo, “Ine sindiri kanthu.” Kotero, inu mukuwona, inu simungakhoze kunena kanthu.

⁴⁰ Tsopano, kwa mzanga wofunika wa Methodisti. Ine ndiri nawo awiri akhala pomwe pano, ndi paliponse. Ine ndiri nawo iwo kunja kuno, ambiri a iwo. Mpingo wa Methodisti unakhulupirira, mmbuyo mu tsiku lake loyambirira, lachikale, kuti, “Pamene munthu ali ndi chipembedzo chokwanira, ndipo wayeretsedwa, akufuula, iye anali nawo Iwo.”

Achipentekoste ankati, “Pamene iye ayankhula ndi malirime, iye anali nawo Iwo.”

Ndipo masiku ano, iwo amati, “Ngati inu muli ndi utumiki wa machiritso, inu muli nawo Iwo.” Koma palibe aliyense wa...

⁴¹ Mvetserani, mzanga. Musati muziyesera kudalira ndi kufuna zogirigisha. Mmalo mwake, muzidalira pa zenizeni, mwaona, osati zogirigisha. Kufuula ndi kwabwino. Kuyankhula mmalirime ndi kwabwino. Kulemekeza Ambuye ndi kwabwino. Chikhulupiro cha zozizwitsa ndi chabwino, zinthu zonsezo.

⁴² Ndipo kumverera kumeneko, ena a iwo amati, “Oh, ine ndinakumverera Iko ngati mphepo yankokomo.” Wina amati, “Ine ndinamverera Moto mu solo yanga.” Chiyani? Zimenezo sizimapangitsa izo kukhala zolondola, mulimonse. Ndi chimene iwe umakhala utatha kulandira icho, mwaona, ndicho chimene chimawerengedwa. Mukuona? Kotero iwe sungakhoze kuwuyika Iwo ku kugirigisha kwina kulikonse.

⁴³ Tsopano, izo nzoona mopambana momwe ine ndikudziwira. Tsopano, ine ndikhoza kulakwitsa; ngati ndikutero, ndiye kuti sindikulimvetsa Lembu. Ndipo ngati izo ziri zotsutsana, chabwino, ine sindikutanthauza kuti ndikhale wotsutsa. Mukuona? Koma ine ndikungonena kugamula kwanga kwa zomwe ine ndikukhulupirira kuti izo nzoona.

⁴⁴ Tsopano, ife tatenga nthawi yathu yochuluka pano pa izi, ife tisanayambe kulowa mu msonkhano wanthawizonse. Ndipo tsopano—tsopano, ife sitimazitchula zinthu izi kawirikawiri pozungulira kachisi, nthawizina. Iyi yakhala nthawi yoyamba, ine ndikuganiza, kwa nthawi yaitali, kwa mwinamwake chaka kapena ziwiri, kapena chinachake. Ndiyeno mwinamwake ena a anthu athu amabweramo, ndipo iwo amati, “Chabwino, M’bale Branham, ine nda—ine ndakhalapo ndi milomo yachibwibwi. Ndipo ine ndachitapo *izi*. Ine ndachita *izo*.”

Ine ndanenapo kuti, “Chabwino, chabwino. Zimenezo ndi zabwino kwambiri.”

⁴⁵ Tsopano, ngati inu mukufuna kuyankhula mu lirime losadziwika, ine ndikukhulupirira Mulungu adzakulolani inu kuti muchite zimenezo. Koma molingana ndi Malemba, inu simuli kanthu mpaka Mzimu Woyera utabwera.

Ndiye, Mzimu Woyera ukadzabwera, ndiye inu mukhoza kudzayankhula mmalirime ndi kukhala... Mulungu adzangotenga chikhalidwe chimene inu muli, ndi kukudulirani inu chimenecho, ndi kudzakupangani inu wantchito wopambana yemwe inu mungakhoze kukhala. Iye akhoza kudzakupangani inu kulalikirira Uthenga. Iye akhoza kudzakupangani inu kukhala ndi mphatso ya kuyankhula mmalirime. Iye akhoza kudzakupangani inu mneneri. Iye akhoza kudzakupatsani inu mzimu wa uneneri. Iye akhoza. Nzovuta kunena, zimene Iye adzakuchitireni inu. Kapena, Iye akhoza kudzakuchitirani inu zinthu zonsezo. Koma chinthu choyambirira, ndi kukhala wotsimikiza, kuti, “Mwa umodzi...” Osati zogirigisha. “Koma mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi

limodzi.” Ndiyeno mphatso zimabwera kuchokera mu Thupi limenelo, mwaona, kuyankhula mmalirime ndi chirichonse.

⁴⁶ Chimene icho chiri, ngati—ngati a Nazarene abwera kwa ine. Inu mungati, “M’bale Branham, tsopano, pali wa Nazarene ndi wa Methodist. Iwo amati iwo analandira Mzimu Woyera pamene iwo anafuula. Iwo anati iwo analandira Mzimu Woyera.” Ine sindikunena kuti iwo sanatero.

Koma pano pali chinthu chimodzi chimene ine ndimawona, “Ndi chipatso chawo.”

Pamene Choonadi chawululidwa, ena a iwo amatenbenukira motsutsa Ichu, mowawa, “Ameneyo ndi mdierekezi.” Ndiye, chipatso chimasonyeza kumene ichu chinachokera. Mukuona? Ichu chimasonyeza kuti iwo sanachipeze Ichu. Koma iwo amene ali ololera kuti ayende mu Kuwala, kulandira Mawu.

⁴⁷ Kuno nthawiyina kale, ine ndinali kulalikira uko mu Kentucky. Ndipo kunja kwa msonkhano, kunali bambo amene anali wa mpingo umene amakhulupirira kuti masiku a zozizwitsa anapita. Iye anali atagwirizira nyali mdzanja lake. Ndipo iye anati, “Ine ndimangokudikirira iwe, mlaliki.” Amalume achikulire ndi ine, amene anapita tsopano.

Ndipo ine ndinati, “Inde, bwana.”

Iye anati, “Ndine *wakuti-ndi-wakuti*.”

Ndipo ine ndinagwedeza dzanja lake. Ine ndinati, “Ndine wokondwa zedi kukumana nanu, m’bale wanga.”

Ndipo iye anati, “Ine ndikungofuna kuti ndikuuzeni inu kuti ine ndikukhulupirira kuti inu mukulakwitsa mwamtheradi.”

Ine ndinati, “Chabwino, inu muli nawo ufulu woti muchite zimenezo, chifukwa ndinu wa Chimerika.” Ndipo iye anati... Chabwino, inu mukuona, ndipo ife tiri... ine ndinati, “Zolakwika pa chiyani? Kodi inu mukanatanthauza pa machiritso?” Ine ndinati, “Nanga bwanji mtsikana wamng’ono ameneyo wopanda nsapato yemwe anangoyenda kupita kumeneko dzulo, usiku watha, anali ndi mwana wamng’ono?”

Iye sanali wopitirira pafupifupi usinkhu wa zaka fortini, iyemwini, wosavala nsapato. Wokalamba wamng’ono... Kodi mumachitcha chiyani chimenecho? Gingham, kaliko, kapena mtundu wina wa diresi. Ine sindimadziwa za nsalu. Ndipo—ndipo iye anali ndi mwana wamng’ono mu dzanja lake, ndipo iye anayenda kubwera kwa ine. Ndipo anthu akumatirira mu win... Ndipo uwu unali mpingo wa Methodist, mpingo wa White Hill Methodist, wochokera ku Burkesville, Kentucky, kumene ine ndinabadwirako. Ndipo iye anali ndi mwana wamng’ono uyu. Ndipo ine ndinati, “Mlongo...”

Ine ndinali nditafunsa, “Aliyense akudwala?”

Ndipo iye anayenda mpaka kumeneko, kanthu kakang'ono, kamanyazi, mutu wake waung'ono uli pansi. Ndipo iye anati, "Inde, bwana, mwana wanga." Ndipo kanthu kakang'onoko kanali kakuyenda monga *choncho*.

Ine ndinati, "Chavuta ndi chiyani ndi iko, mlongo?"

Iye anati, "Iko kali ndi zodzigwedeza."

Ndipo ine ndinati, "Zodzigwedeza?"

"Inde, bwana."

Ine ndinati, "Kodi iko kakhala nazo nthawi yayitali bwanji?"

Ndipo iye anati, "Chabwino, kuyambira pamene iko kanabadwa, ndipo izo zikhoza kukhala pafupifupi usinkhu wa chaka."

Ndipo ine ndinati, "Kodi inu muli wololela kundilola ine kuti ndimugwire mwana ameneyo?" Kumtunda uko mmapiro umayenera kukhala ngati ukuyang'anitsitsa za zimenezo.

Ndipo iye anati, "Inde, bwana." Iye anamupereka munthu wamng'onoyo mdzanja langa.

⁴⁸ Mu mtima mwanga, ine ndinangoima njii, miniti. Ine ndinati, "Mulungu, ngati Inu mungandilole ine kuti ndiwapindulire anthu awa, ndiye mundichitire ine chinachake tsopano."

Ndipo pamene ine ndinali kukagwira iko m'dzanja langa, iko kanasiya kugwedezeke. Ine ndinayang'ana pa iko. Ndinakakhazika iko, mmikono, ndinasewera nako iko, ndipo iko kanamwetulira ndi kundiseka ine. Ine ndinayang'ana pansi pa iye. Ndipo iye anadzutsa... Anali ndi mutu wake wawung'ono pansi, tsitsi lake linagawanika ndi kulendewera pansi pa nsana wake, ndi zomanga pa ilo. Iye anadzutsa mutu wake mmwamba, ndipo misonzi ikutsikira pansi mmasaya ake aang'ono. Amuna aukali atayima pamenepo, ndevu pa nkhope zawo, motalika *choncho*, ndi misonzi ikuyenderera pansi pamasaya awo. Ndinayang'ana pozungulira. Ine ndinati, "Mwana wanu ndi uyu, mlongo. Yesu Khristu wamuchiza iye." Ndipo akazi achikulire amenewo anayamba kukomoka ndi kugwera pansi, ndi kuthira madzi mu nkhope zawo, ndi kumawakupiza iwo.

Ndipo—ndipo, bwanji, ine ndinati, "Nchiyani chinachita zimenezo?"

Iye anati, "Bambo Branham, ine sindingakhoze kuvomereza chirichonse mpaka ine nditachiwona icho bwinobwino."

Ine ndinati, "Chabwino, lingaliro labwino, ine ndikuganiza. Koma," ine ndinati, "Ine ndikufuna ndikufunsemi inu, inu mumakhala kuti?"

Iye anati, "Kuseri uko kuwoloka phiri kuno, kutali. Mupite kunyumba ndi ine ku chakudya chamadzulo usikuuno, ndipo ine ndikakupatsani inu mkaka wina ndi mkate wa chimanga."

Ine ndinati, “Ine ndingakonde kuti ndipiteko, ndipo ine ndiri ndi njala kwenikweni, koma,” ine ndinati, “Ine sindingachite zimenezo. Ndiyenera kupita kunyumba ndi amalume anga.” Ndipo iye...Ndinati, “Chabwino, ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu—ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake. Inu mukudziwa bwanji kuti mukafika kwanu?”

Iye anati, “Chabwino, ine ndingoyenda kuwoloka phiri limenelo.”

Ine ndinati, “Kodi mukukhoza kuwona kwanu?”

Iye anati, “Ayi.”

Ine ndinati, “Ndiye inu mukudziwa bwanji kuti inu mukafika kumeneko?”

Iye anati, “Pali njira imene imapitako.”

Ine ndinati, “Koma, apobe, inu simukukhoza kuyiwona iyo. Ndipo inu mwangondiuza ine kuti simungakhoze kuvomereza chirichonse kupatula inu mutachiwona icho, bwinobwino.”

“Oh,” iye anati, “Ine ndingotenga nyali ndipo ndiziyenda ndi kuwalako.”

Ine ndinati, “Ndicho basi chimene ine ndikuyesetsa kuti ndikupangitseni inu kuti muchite.”

Basi pamene nyali ikupereka kuwala, inu muziyenda mu Kuwala pamene Iye ali mu Kuwalako. Ife tikafika kumeneko mwabwino. Ngakhale ine sindikuwona mapeto, bwinobwino, koma ine ndikudziwa kuti iwo adzakhala alipo.

Tiyeni tipemphere tsopano.

⁴⁹ Atate Akumwamba, ndife oyamikira kwa Inu chifukwa cha ubwino wa Yesu Khristu, Amene ali chirikati cha chikondi. Ndipo ine ndinkakonda kuganiza kuti Inu munandikwiya ine, koma Yesu amandikonda ine. Koma ndinadzapeza tsopano kuti Yesu ndi mtima kumene wa Mulungu, kotero ine—ine ndikudziwa kuti Inu mumandikonda ine ndipo—ndipo munavutika chifukwa cha ine.

⁵⁰ Ndipo, Atate Mulungu, ine ndikupempherera dziko lino lero, ndi dziko lathu. Ine ndikupemphera, Ambuye, kwa chikhululukiro cha zolakwitsa zanga zomwe ndi kwa zolakwitsa za anthu anga, anthu amene Inu mwandipatsa ine kuti ndikhale m’busa wawo. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu muwadalitse iwo, ndi mmodzi aliyense wa anthu amene akhala ali mu msonkhano waung’ono uno, amene afunsa mafunso. Kapena—kapena, mwinamwake ine ndanena chinachake chosiyana ndi chimene iwo amachikhulupirira. Ambuye, ine sindingathe kuzifotokoza izo, inemwini. Ndine wosatha. Koma mulole...Kodi Inu mungangowadziwitsa iwo, Atate, kuti mu mtima mwanga, chimene ine ndikutanthauza?

Chonde. Ine ndikupemphera Inu muchite zimenezo. Adalitseni iwo, pamodzi.

⁵¹ Tidalitseni ife tsopano pamene ife tikuyembekezera pa Mawu Anu, mphindi pang'ono chabe utumiki wa ubatizo usanachitike. Tithandizeni ife kuti tiziyankhula izo zomwe ziri zolondola. Tithandizeni ife, mu Uthenga uwu usikuuno, kumero kwanga pokhala kuti kwasasa pang'ono. Ine ndikupemphera kuti Inu mundithandize ine, wokonedwa Mulungu, ndipo Inu mudzachiritse ngakhale odwala ndi osautsika amene ali pakati pa anthu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

⁵² Tsopano, ngati mungathe, kwa mphindi pang'ono chabe zotsatirazi, tiyeni titembenuzire ku Bukhu la Aroma, mutu wa 6.

Oh, dikirani. Ine ndikukhulupirira ine ndiri nazo... Ndikuti, ine ndiri ndi mafunso ambiri... Ndimati, ine ndidzangowayankha awa Lachitatu lino usiku, ngati izo ziri bwino. Ine ndathedwa, ndachedwa kwambiri tsopano. Ine sindinawawone awo amene ali apowo mpaka pakali pano.

Tsopano, Aroma mutu wa 6, tiyeni tiwerenge.

Kodi ife tidzanena chiyani ndiye? Kodi tidzapitiriza mu tchimo, kuti chisomo chikhoze kuchuluka?

Mulungu aletse. Kodi ife amene tinafa ku tchimo tidzakhala motalika bwanjinso mmenemo?

Kodi inu simudziwa, kuti ambiri monga... a ife monga anabatizidwa kwa Yesu Khristu anabatizidwa ku imfa yake?

Chotero ife tinaikidwa mmanda limodzi ndi iye mu ubatizo kwa imfa: kuti monga momwe Khristu anaukitsidwira kwa akufa mwa ulemelero wa Atate, ngakhale ife tiziyenda mu utsopano wa moyo.

Pakuti ngati ife tinabzalidwa limodzi m'chifaniziro cha imfa yake, ife tidzateronso mu chifaniziro cha chiukitsiro chake.

⁵³ Ngati ine ndingatenge phunziro usikuuno, kwa pafupifupi maminiti twente, Ine ndinganene ichi, “kuzindikiritsidwa,” Kuzindikiritsidwa Ndi Khristu.

⁵⁴ Inu mukudziwa, ziripo, mdziko lero, anthu ambiri ndi osakhutitsidwa. Ndipo ndi zodabwitsa, pamene iwe uyenda ndi kupeza kusakhutitsidwa kochuluka. Anthu sakudziwa nkomwe zomwe iwo akufuna kuti achite. Iwo amabwera akuyenda pa msewu pafupifupi mailosi sevente ndi eyite pa ora, mu dera la mailosi sarte; kukhwekheretsa mabureki ndi kuzungulira ngodya, ndi kuwuyamba ndi liwiro loterolo mpaka kuwotcha matayala awo, kuti apite ku mdadada wa mzinda, kukakhala

pansi ndi kukacheza pang'ono. Zikuwoneka ngati anthu sakudziwa chimene iwo akuchifuna.

⁵⁵ Ena a iwo amasokonezeka kwambiri mpaka iwo amapita kumalo ogulitsira mankhwala ndi kukadzigulira okha botolo la arseniki, chidulo cha safuriki kapena chinachake, ndi kudzipha okha. Iwo amawapeza iwo atagona akufa. Ena amayatsa ma mapaipi awo a gasi mchipinda, kapena amakhala mmagalimoto awo ndi mapaipi a gasi wa carbon monoxide, kuyesera kuti achoke m'moyo. Ena a iwo amakwera mpaka pa mlatho, ndi kulemba cholemba chaching'ono ndi kuchimata icho pa chikhotho chawo, ndi kuchiyika icho pansi, ndipo nkudziponyera okha ku imfa mu mtsinje; kulumpha kuchoka ku mapiri, nsanja zazitali. Ndipo ena amatenga mfuti ndi kuiyika iyo pa mutu wawo, ndipo kwenikweni nkuphulitsa ubongo wawo. Iwo ndi osakhutitsidwa basi.

⁵⁶ Mzipatala ndi modzaza ndi anthu osakhutitsidwa. Malo osungira amisala ndi mosefukira. Osakhutitsidwa! Iwo sakudziwa zimene iwo akufuna. Zikuwoneka kuti pali chinachake chomwe iwo akuchifikira, koma iwo basi samabwera kwa icho.

⁵⁷ Ndiponso ife tikupeza kuti, m'mabanja, zomwe ziri nsana wa fuko ndi—ndi wa mpingo, tikupeza kuti mabanja asweka, ndipo mabwalo amilandu azilekano angodzaza ndi zilekano. Kupanda khalidwe kwa ana, za—za amayi kuwasiya ana awo aang'ono ndi owalera ndi—ndi kumachokapo, kumapita ku ntchito ndi kwinakwake, pamene amuna awo ali ndi ntchito zabwino, koma iwo sakukhutitsidwa basi kukhala mayi ndi kukhala pakhomu. Iwo sakukhutitsidwa kuti azivala monga madona. Iwo—iwo akufuna kuti azivala monga amuna. Amuna akufuna kuti azikhala monga akazi. Ndipo iwo basi... Apo zikungowoneka kuti pali chinachake cholakwika, penapake. Ndipo anthu akufikira chinachake, ndipo sakukhoza kuchipeza icho. Ndicho chikhalidwe chomvetsa chisoni kuti ukhalemo.

⁵⁸ Iwo ayang'ana paliponsepo, kuti apeze chinachake, kuti adzipange iwoeni chitsanzo. Ife tiwatenge akazi a tsiku lathu, iwo amakawonera televizioni mpaka iwo amamuwona katswiri winawake wa pakanema. Kapena, iye amatulukako, atavala mwanjira inayake, ndipo akazi onse amafuna kuti azivala monga iyeyo, kapena kumachita monga iyeyo, kumupanga iye kukhala chitsanzo. Atsikana ena okongola, basi mu kuphukira kwa moyo, amayesetsa kuti adzifanizitse okha, ndi kuyesetsa kupanga katswiri wa pakanema kukhala chitsanzo chimene iwo aziyendera nacho. Ndipo potsiriza iwo amadzipeza okha atamangidwa mu khola la tchimo lomwe iwo sangathe kuchokamo. Ndi zachisoni bwanji! Kuwawona iwo akubwera mu msonkhano, misonzi ikutsikira pansi mmasaya mwawo, koma iwo akusaka chinachake.

⁵⁹ Ife tiwatenge amuna. Amuna, inu mukawapeze iwo pa msewu kapena mmageni awo. Bambo wachikulire akufuna kuti akhale wachinyamata. Iye amameta tsitsi lake, pamwamba pake, ndi kupanga ka—kachipsyepsye ka bakha kumbuyo. Iye akufuna kuti akhale wachinyamata. Wachinyamata amafuna kuti akhale ngati mmodzi wa mfumu ya gwedemula iyi. Kodi iwo amakathera kuti? Mu tchimo ndi chitonzo.

⁶⁰ Munthu akuwoneka kuti sakukhutitsidwa. Iye akuthamanga konsekonse. Iwo akumatengeka ndi... akumakamvetsera wailesi, kufuna nthabwala ndi zinthu zomwe anthabwala awa amanena. Ndipo iwo amatuluka ndi kukayesera kutsanzira kapena—kapena kukachita monga anthu amenewo.

⁶¹ Inu mumutenge mnyamata wamng'onoyo pa msewu. Momwe ine ndimadziwira izo! Ndipo iye ayenera kukhala Womenyera chirungamo, kapena Hopalong Cassidy. Kapena... Ndipo dziko lamalonda limamutenga ameneyo ndipo limapanga mamillioni a madola kuchokera mwa zimenezo. Iwo ayenera kukhala Roy Rodgers, kapena a—a Bambo Dillon, kapena—kapena wina wa pa purogramu ya televizioni.

Iwo akuyesetsa kuti amutsanzire munthu ameneyo. Iwo amawayika iwo ngati chitsanzo. Iwo awatenga iwo kukhala—muyezo wawo wa moyo. Ndipo kodi iwo akumapeza chiyani kumapeto kwa msewu? Ana aang'ono amenewo akumasanduka kukhala zigawenga ndi achifwamba. Akazi akumasanduka kukhala mahule, ndi—ndi oyenda pamsewu, ndi—ndi anthu opulikira. Amuna akumasanduka kukhala ochita juga, ndi, “Okonda zosangalatsa kuposa kukonda Mulungu.” Mipingo ikumayesetsa kutsanzira mpingo winawo, mpingo wawukulu.

⁶² Ife tikungowoneka kuti tikuwona, palibe kukhutitsidwa pakati pa anthu. Kodi iwo akuchita chiyani... .

Nchiyani chikuwapangitsa iwo kumachita zimenezo? Ndi kwa cholinga. Ndi chikhalidwe. Mulungu anawapatsa iwo chikhalidwe chimenecho. Iwo ali ndi chikhalidwe chimene chimawapangitsa iwo kufuna kukhala ndi chinachake choti azidzizindikiritse nacho okha. Iwo ayenera kukhala ndi chinachake chimene amafuna kuti azifanana nacho, cholinga mmoyo.

Iwo amafuna kuti akhale katswiri wa pa kanema, kapena wolishya ng'ombe, kapena—kapena chinachake pa lingaliro limenelo.

⁶³ Ine ndinali kumva pa wailesi, ndikubwera kunyumba, kumene munthu wina wotchuka wa ku Italy, ku Denver, anali kuyesetsa kuti azichita za Hopalong Cassidy, chinachake, ndi mfuti yolongedza. Ndipo mmalo mwa zimenezo, iye adzakhala Chester, moyo wake wonse. Iye anadziwombera bondo lake. Ndi zimenezotu pamenepo.

⁶⁴ Koma iwo akuyesetsa kuti apeze chinachake choti azidzizindikiritsa nacho okha. Chifukwa chimene iwo akuchitira zimenezo, ndi chifukwa chakuti muli chinachake mwa iwo, ndipo Mulungu anawapanga iwo chimenecho.

Koma Mulungu anawapangira iwo chitsanzo choti azizindikiritsidwa nacho, ndipo icho chinali pamene Iye anamupanga Yesu Khristu kuti akhale Mpulumutsi wanu. Ndicho chitsanzo. Ndicho chimene anthu akufuna, ayenera kuzindikiritsidwa ndi Yesu, kuti akhale monga Iye.

⁶⁵ Ngati anyamata aang’ono onse amene amafuna kukhala Hopalong Cassidy kapena—kapena ena a ena awa; kapena atsikana aang’ono, a Annie Oakley ndi ena otero; ngati iwo akanangofuna kukhala monga Yesu, mochuluka momwe iwo amafunira kukhala monga choncho, ma Sande sukulu akanakhala akusefukira, konsekonse. Ngati akazi amene amafuna kuti akhale monga katswiri wina wapa kanema, akanafuna kukhala monga Yesu, mpingo, bwanji, iwo sibwenzi akuchita kutenga chopereka. Ndithudi.

⁶⁶ Mulungu anamupanga munthu kuti azikhumba kuti akhale ndi chitsanzo. Ndipo Mulungu anamupatsa iye chitsanzo. Chitsanzo chimenecho ndi Yesu Khristu, kuti azizindikiritsidwa ndi Iyeyo.

⁶⁷ Tsopano, ngati tikanakhala mochuluka monga Iye, ndiye sibwenzi tiri ndi mabwana-akuluakulu mdziko. Sipakanakhala ana anjala aliwonse mdziko. Sipakanakhala kachasu aliyense, kapena kumwa, kapena kuchita juga. Mulungu anatipatsa ife chitsanzo kuti tizifanana naye, koma timakana kukhala chimenecho. Tsopano, ndiro limene liri vuto ndi dziko. Iwo ali nacho chokhumba, Mulungu wawapatsa iwo chimenecho, koma iwo achikana icho mwanjira yolakwika. Ndi nthawi yobwerera ndi kukalowa pa njira yoyenera, ndi kukayang’ana pa Gologota. Chirengedwe chimatsimikizira zimenezo.

⁶⁸ Tsopano, ngati anthu a tsiku lino, ndi chokhumba chachikulu chimenecho ndi kulakalaka kwakukulu kuti akhale monga winawake, ngati chitsanzo. Ngati iwo akanamutenga Khristu ngati chitsanzo chawo, ndiye ife tikanakhala...Ife tikanakhoza kumuchotsa wapolisi aliyense yemwe analipo, mu fuko. Aliyense akanakhala wofatsa ndi wodzichepetsa. Aliyense akanakhala wachifundo ndipo akanakhala ndi chikondi cha pa abale, wina kwa mzake. Sibwenzi pali mlandu wa chilekano umene ukananenedwa mdziko lathuli. Sibwenzi pali matenda aliwonse. Ife tikanakhoza ngakhale kuzithetsa zipatala, ngati aliyense akanayesera kumupanga Yesu Khristu chitsanzo chawo. Ife sibwenzi tikusowa kanthu kalikonse.

⁶⁹ Chotero, chikhalidwe chimenecho chiri mwa munthu, koma iye amachiyika icho pa chinthu cholakwika. Iye amamupanga munthu winawake...Ndipo inu mukudziwa, Baibulo linanena,

kuti, “Ife timakhala otembereredwa pamene ife tipanga thupi pokhalapo pathu. Pamene inu muyesera kupanga thupi kukhala pokhalapo panu, kapena kuika chidaliro chanu mu thupi,” Baibulo linati, “ndinu otembereredwa.”

Momwe ndikudziwira bwino! Ndi zophweka kuti uchite zimenezo.

⁷⁰ Izi ndi zomwe zimayambitsa zambiri za izo, ndi zolemba nkhani zathu zodzaza ndi magazini onyansa; nyumba zathu zadzaza ndi zithunzi zomata-mata. Zowonera nkhani zathu sizikuwunikidwa; izo zikumakhala zotseguka, akhoza kuswa nthabwala ya mtundu uliwonse, kapena—kapena kuchita zinthu zimene ziri zoipa. Palibepo chiyeo pakati pathu, panonso. Ine ndikudziwa inu mukuganiza kuti ndine wovuta kwambiri pa zimenezo. Koma ndi... Winawake ayenera kukhala wovuta pa izo. Izo zikungoyenera kuchitidwa.

⁷¹ Pamene ine ndinali mnyamata wamng’ono, ine ndinawerenga bukhu la *Tarzan, Apes*. Amayi anali ndi chiguduli chakale chaubweya chimene Akazi a Wathen anawapatsa iwo, anachiyika patsogolo pa choika zovala. Ine ndinachidula chinthu chimenecho ndipo ndinadzipangira ine suti ya Tarzan, ndipo ine ndinagona mu mtengo kwa sabata. Ine ndimafuna kuti ndikhale Tarzan. Ndiye pamene ine ndinadzawerenga bukhu la *The Lone Star Ranger*; ine ndinkakwera ndodo yatsache, kukhala khalidwe la kavalo, kuyesetsa kuti ndikhale Lone Star Ranger.

⁷² Si zoposa zimene anthu ati adzachite. Ndi zimene inu mumawerenga, nyimbo zimene inu mumamvetsera.

Kupita kumalo odyera, ndipo gwedemula wakale uyu, nzosadabwitsa kuti anthu achita misala. Izo ndi zokwanira kumuchititsa munthu misala.

⁷³ Koma, oh, ine ndidzakhala wothokoza, monse kudutsa mu Muyaya, kudzafika tsiku lina ine ndinawerenga za Yesu. Zimenezo zinandikhutitsa ine. Ine ndikufuna kukhala monga Iye. Ndicho chokhumba changa, kuti ndidzakhoze kutembenuza tsaya linalo, kapena kupita mtunda wachiwiri. Kuti ndidzakhoze kukhululuka, pamene zopinga zonse zikukutsutsa iwe, osasunga mangawa ndi aliynse. Ngakhale iwo akukuchitira iwe nkhanza moyenerera, kapena molakwika chifukwa chakuchita bwino kwako, koma nkumawakondabe iwo. Ndi momwe ndikufuna kumakhalira. Ine ndikufuna kuti ndikhale munthu wa mtundu umenewo. Ine ndikufuna kuti ndidzakhoze kukwanitsa, kuti, pamene ine ndikunyozedwa, ndisanyoze mobwezero. Ndiwo mtundu wa chitsanzo chimene Mulungu anatipatsa ife mwa Yesu Khristu. Ife tiyenera kuzindikiritsidwa ndi Iyeyo. Ife tiri ozi-...

⁷⁴ “Iwe umadzakhala wozindikiritsidwa ndi Iye chotani,” inu mungatero, “M’bale Branham? Tsopano, kuti titenge...”

inu mumayenera kumavala monga nyenyezi za ku Hollywood ndi kumachita zinthu zina izi. Koma iwe ungakhale bwanji wozindikiritsidwa ndi Yesu Khristu?"

Choyambirira, iwe ulape za zimene inu unachita kale. Ukatero iwe umazindikiritsidwa ndi Iye, apa mu dziwe. Nzosakaikitsa koma kuti ambiri adzazindikiritsidwa ndi Iye, mu maminiti pang'ono. Mu dziwe, iwe umazindikiritsidwa ndi Iye mu ubatizo. "Pakuti ngati ife taikidwa mwa Khristu, ife timazindikiritsidwa ku imfa Yake, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro." Ndi chifukwa chake ife timabatizidwa. Ife timapita pansi mmadzi, nkubwereranso kudzachitira umboni kuti ife tikukhulupirira mu imfa, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro cha Yesu Khristu. Ndipo ngati ife titabzalidwa mmawonekedwe Ake, mu imfa Yake, Mulungu anatipatsa ife lonjezo: ife tidzakhala monga Iye, mu chiwukitsiro.

⁷⁵ Muzizindikiritse nokha ndi katswiri wina wa pa kanema, ndipo muwone kumene inu muti mudzakhale. Muzizindikiritse nokha ndi wolishya ng'ombe wina, kapena wachinyamata wina, ndipo muwone kumene inu muti mudzakhale.

Koma ine ndikukubetcherani inu, usikuuno, muzizindikiritse nokha ndi Yesu Khristu, mu imfa Yake, mu chiwukitsiro Chake, ndipo muwone kumene inu muti mudzakhale pa chiukitsiro. "Pakuti ngati ife tivutika ndi Iye, ife tidzalamulira limodzi ndi Iye." Mulungu watipatsa ife lonjezo. Chokhumba changa chonse ndicho kukhala monga Iye.

Nditengeni ine, O Ambuye, ndipo mudiwumbe ine ndipo mundipange ine. Mudiwumbenso ine. Monga mneneri amene anatsikira ku nyumba ya wowumba mbiya, mundiphwanye ine ndipo mudiwumbenso ine.

⁷⁶ Mu Chipangano Chakale, pamene munthu akafuna kuzindikiritsidwa pa nyumba ya Mulungu, iye ankatenga chinthu chosalakwa kwambiri chimene iye akanakhoza kuchipeza, mwanawankhosa. Ndipo iye ankadziwa kuti mwanawankhosa anali mfulu kwa tchimo, chifukwa iye sankadziwa ayi tchimo. Ndipo iye ankapita, ndipo ankakatenga mwanawankhosa, ndi kuyika dzanja lake pa mutu wake, ndipo ankavomereza machimo ake. Ndipo mwa chikhulupiro, iye ankasamutsa machimo ake pa mwanawankhosa, ndipo kusalakwa kwa mwanawankhosa kunkabwerera pa iye. Ndiyeno mwanawankhosa ankafa, chifukwa iye anali wochimwa. Ndipo munthuyo ankakhala moyo, mwa kuchita kwa chikhulupiro, pomvera zomwe Mulungu ananena. Koma kodi iye amachita chiyani? Iye ankabwerera kumene kuchokera mu kachisi, ali ndi chikhumbo chomwecho chimene iye anali nacho pamene iye amabwera mmenemo. Chifukwa, pamene khungu la magazi limenelo lisweka... Chimene, moyo umayambira mu khungu limodzi la magazi. Ndipo pamene khungu la magazi limenelo

linaswedwa, moyo wa mwanawankhosa sukanagwirizana, kapena kubwereranso mu moyo wa munthu, chifukwa iwo unali moyo wa chinyama. Munthuyo amatuluka panja ndi chikhumbo chomwecho chimene iye anali nacho, chotero choncho iye amachita machimo mosalekeza, nthawi zonse, kachiwiri.

⁷⁷ Koma inafika nthawi pamene Mulungu anatipanga ife chitsanzo, ndipo Iye anatipatsa ife Ambuye Yesu. Ndipo pamene wochimwa ayika manja ake pa mutu Wake wofunika, ndi kuvomereza machimo ake, ndipo machimo ake amasinthidwa kapena—kapena amatsamutsidwa kuchoka pa wochimwa kupita kwa Yesu; ndipo kusalakwa kwa Yesu kumasamutsidwa, mwa Mzimu Woyera, kubwerera mwa munthu ameneyo. “Iye ndi cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu.” Ndi pamene ine ndikufuna kuti ndizindikiritsidwapo. Baibulo linati, “Iye, asakudziwa tchimo, anapangidwa tchimo chifukwa cha ife.” Chifukwa chimene Iye anamva kuwawa chinali cha machimo athu. Ndipo sizoposa chimene chiri cholondola, monganso ntchito yathu ili kuyang’ana pa zinthu izi ndi kumawona kuti zokhumba izi zimene ife tiri nazo, zimene Mulungu anaziika mwa ife, kuti alenge mwa ife, kuti atipange ife kuti tizifuna kukhala monga Iye.

⁷⁸ Ndipo tsopano, ngati inu mungakhoze kuziwona izo, mwa chikhulupiriro, chikhumbo chenicheni chisanakukhudzeni inu, bwerani patsogolo, mudzazindikiritsidwe ndi Iye mu ubatizo. Ndiyeno monga mukubzalidwa mu chifaniziro cha imfa Yake, inu mudzakhalanso mu chifaniziro Chake, mu chiukitsiro. Pakuti pamene Iye anabwera kuchokera mmanda, Iye anali Yesu yemweyo amene anapita mmanda. “Ndipo ngati ife tiri mwa Khristu...” Ife timalowamo chotani? Mwa ubatizo wa Mzimu Woyera. “Pa tsiku limenelo ife tidzabwera ndi kudzagawana mu chiwukitsiro Chake.”

Panali nyimbo yaying’ono imene ine ndinkakonda kuyiimba, zaka zapitazo:

Kukhala monga Yesu, kukhala monga Yesu,
Padziko ine ndikufuna kukhala monga Iye;
Monse kupyola ulendo wa moyo kuchokera
padziko kupita ku Ulemelero
Ine ndikungopempha kuti ndikhale monga Iye.
Kuchokera ku khola la Betelehemu kunabwera
Mlendo, (Mlendo, kwa dziko.)
Padziko lapansi ine ndikufuna kukhala monga
Iye;
Monse kupyola ulendo wa moyo kuchokera
padziko kupita ku Ulemelero
Ine ndikungopempha kuti ndikhale monga Iye.

⁷⁹ Kugawana mu kufatsa Kwake, inu mudzagawana nanunso mu mphamvu Yake. Kugawana mu kumvera Kwake, ndipo inu

mudzagawana mu chiwukitsiro Chake. Muzichita monga Mulungu anati muchitire. Mu mtima mwanga, chinthu chachikulu chimene ine ndingakhoze kuchiganizira, ndi kukhala monga Yesu Khristu, kuti ndizizindikiritsidwa ndi Iye. Ndi chifukwa chake ine ndimawabatiza anthu mu Dzina la Yesu Khristu, chifukwa Iye ndi chotizindikiritsa chathu. Iye timanyamula chizindikiritso. “Chirichonse chimene inu muchita mu mawu kapena mu ntchito, muzichichita icho mu Dzina la Yesu Khristu, kupereka matamando kwa Mulungu chifukwa cha zimenezo.” Ndipo ife timazindikiritsidwa ndi Iye mu ubatizo.

⁸⁰ Usikuuno, ife tibatiza, mu maminiti pang’ono chabe, anthu muno mchipinda, amene ali pano kuti abatizidwe. Ndipo ngati muli chikhumbo chirichonse mu mtima mwanu, chimene inu mukufuna, muli ndi chikhumbo chachikulu chachidziko chirichonse, mulape za izo pakali pano. Mumuuzo Mulungu kuti inu mukupepesa kuti inu mumafuna kuti mukhale munthu wina wamkulu wa chidziko. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Munene kuti, “Ambuye, chokhumba changa chathunthu ndicho kukhala monga Yesu.” Mubwere mofatsa, modzichepetsa. Ndiye, pamene mukuyika manja anu pa Mutu Wake, ndipo mwa chikhulupiriro muvomereze tchimo lanu, munene kuti, “Ambuye, ine ndikupepesa kuti ndinachita izo.” Ndiye nchiyani chiti chidzachitike? Mulungu adzatsamutsira kulakwa kwanu konse pa Iye, ndipo adzatenga kusalakwa Kwake ndi kudzakuika iko pa inu. Ndipo inu mudzaima wolungamitsidwa, mu Kukhalapo kwa Mulungu, chifukwa inu munakhulupirira pa Yesu Khristu, Mwana Wake. Ndi dongosolo bwanji la chipulumutso! Zikadzatero inu mudzagawana mu ulemelero Wake. Ubwino wa Mulungu udzabwera mu mtima mwanu. Mphamvu ya chiwukitsiro Chake idzakupangani inu munthu watsopano. Iyo idzakhutitsa kukhumba kulikonse.

⁸¹ Pamene ine ndinali mnyamata, ine ndinayesera kuchita chirichonse. Ine—ine ndinachita chirichonse chimene ine ndinali wamkulu mokwanira kuti ndichichite, ndi zinthu zambiri zimene ine sindinali wamkulu mokwanira kuti ndizichite, ine ndinayesera. Ine ndinkakonda kukonda, ine ndimakonda, kusaka. Ine ndinkaganiza kuti zinali zimenezo. Ine ndinkaganiza ngati ine... Abambo anga anali wokwera. Ndipo ine ndinkaganiza, “Ngati ine ndikanati ndidzafike konse Kumadzulo ndi kukawaphunzitsa akavalo awo!”

Koma, m’bale, nthawi ina kutali komwe uko mu mapiri mu Arizona, ndikubweretsa gulu la ng’ombe, usiku wina. Ine ndinali nditakhala pamenepo. Ndipo mnyamata dzina lake Slim anali ndi chipeso chakale, chiri ndi chidutswa cha pepala pa icho. Iye anali kuyimba. Munthu wina atakhala pamenepo, wochokera ku Texas, ali ndi gitara, akuikhwatcha. Ndipo iwo anafika pa nyimbo. Ine ndinachotsa chishalo changa pa kavaloyo; kugoneka

pansi mutu wanga, kuchigwiritsa icho ntchito ngati chotsamira. Ndipo bulangeti langa liri pamwamba pa ine, ndi ine mmenemo, ndipo ndiri chivalireni nsapato zanga, magudumu azisonga akundigwira ine kuti ndisagwere pansi. Ndipo iye anayamba kukhwatcha:

Pansi pa mtanda pamene Mpulumutsi wanga
anafera,
Pansi apo ponditsuka ku tchimo ndinalira;
Pomwe mtima wanga Magazi anapakidwa;
Ulemelero kwa Dzina Lake!

⁸² Ine ndinayesera kukokera bulangetilo mmwamba, ndi kuyimitsa makutu anga mmwamba. Ine ndimakhoza kuyang'ana mmwamba, ndipo nyenyezi zikulendewera pansi. Ndipo mapaini onong'ona amenewo mmapiri ankawoneka ngati akulira, "Adamu, iwe uli kuti?"

Oh, kuweta ng'ombe chinali chinthu chachiwiri. Ine ndinkafuna kuti ndimupeze Mulungu. Kumbuyo komwe uko, ndinakwera pa magudumu azisonga zimenezo, Ine ndinati, "Bwana, ine sindikudziwa yemwe Inu muli, koma musati mundilange ine mpaka ine nditapeza chinthu chenichenicho."

⁸³ Masiku awiri zitachitika zimenezo, uko mu mzinda, nditakhala pamenepo, ndipo patapita masiku angapo zitachitika zimenezo, kutatha kukusa. Ine ndinali nditakhala pamenepo pa benchi yaing'ono ya ku paki. Mtsikana wamng'ono wa Chispanishi anabwera pamenepo. Ndipo ine ndinali nditakhala pamenepo, ndikuganiza za Mulungu, "Kodi Ichu chingakhale chiyani?" Mtsikana wamng'ono, wokalamba anabwera, ndipo ine basi pafupifupi mnyamata wa usinkhu wa zaka eyitini. Iye anagwetsa mpango wake ndipo anadzayenda moyandikira. Ine ndinati, "Mkazi, iwe wagwetsa mpango wako." Malingaliro okha a Mulungu anali atasintha chokhumba changa. Mtima wanga wosauka wachi Irish unali ndi njala, ine ndinkafuna chinachake, chinachake chimene chinkakhutitsa.

⁸⁴ Mulungu wandipatsa ine mwayi wosaka dziko lonse: Afrika, India, kudutsa mapiri, Canada, pa maulendo ena akuluakulu, ndi kugwira zodziwika za padziko lapansi. Ndizo zonse, zabwino, koma palibe chimene chiti chidzatenge malo a mphamvu imeneyo ya Mulungu wamoyo ikutsikira mu solo yanu.

⁸⁵ Pamene ine ndidzafike kumeneko, ine ndimakonda mapiri. Ine ndimakonda kulowa kwa dzuwa. Ine basi—ndimangokhoma chikhomo, ndi kumangapo kavalo wanga. Ndi kumakwera, pamwamba pa mapiri, ndi kukakhalako masiku angapo, kumangoyang'ana dzuwa likutuluka ndi kumatsikira pansi, kumamvetsera mphungu ikufuula. Ndi zabwino. Ine ndimakonda kukhala kumeneko. Koma, m'bale, mtima wanga umayamba kumenya ndi kugunda, pamene ine ndiganiza za:

Wosayera! Wosayera! Mizimu yoipa
 inamung'amba iye.
 Zonse ziri bwino pamene Yesu abwera kuti
 adzakhale.

Ine ndimayamba kuganizira za anthu odwala, ndi kuyitana kumeneko. Ndipo pali chinachake mkati mwanga, chimafuula mokweza, “Tsika pansi pa mapiri awa mwamsanga ndithu. Tsikira pansi uko kwa anthuwo.”

Ine ndikufuna kudzizindikiritsa ndekha ngati wantchito Wake pakati pa anthu Ake. Oh, momwe ine ndimakondera kudzizindikiritsa ndekha ndi Iye. Ndiye, polemekeza chimenecho, Iye amabwerera pakati pathu ndipo amadzazizindikiritsa Yekha ndi ife. Iye ali pano usikuuno, mzanga.

⁸⁶ Ndi nthawi tsopano kuti utumiki wa ubatizo uyambe, mu pafupifupi maminiti teni. Ndipo ine ndikufuna kunena chinthu chimodzi ichi ife tisanachite zimenezo, ife tisanayambe iwo. Yesu Khristu Mwana wa Mulungu. . . Ndemanga zambiri basi zimene ine ndikufuna kuti ndinene, koma ine ndiribe nthawi.

Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, wadzizindikiritsa Yekha mu Mawu Ake. Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, wadzizindikiritsa Yekha mu msonkhano mmawa uno, popereka kuzindikira za mumtima. Akudzizindikiritsa Yekha pobweretsa wochimwa kuchokera ku zithaphwi za tchimo, kupita kukakhala munthu watsopano, cholengedwa chatsopano. Kumutenga wotsikitsitsa wa mkazi kapena wotsikitsitsa wa mwamuna, woledzera, chidakhwa, ndi chirichonse chimene chiri, ndi kuwawongola iwo ndi kuwayeretsa iwo, ndi kuwapanga kukhala njonda kapena dona kuchokera mwa iwo. Ameneyo ndi Ambuye wanga. Kumutenga munthu amene akudwala ndi osautsika, ndipo wopanda chiyembekezo kwa iye, ndipo nkumuwukitsira iye ku moyo watsopano kachiwiri. Ndiye nkuwonekera pakati pathu, ndi kudzizindikiritsa Yekha ngati Yesu yemweyo, kudzadziwa malingaliro omwe a mtima wathu. Kudzaima pakati pathu, mwa anthu Ake, Mulungu mwa anthu Ake, akudzizindikiritsa Yekha. Iye ali pano tsopano, Mzimu Woyera womwe uja.

⁸⁷ Ife tisanayambe msonkhano umenewo muno wa ubatizo, pamene abale akukonzekera, ine ndikudabwa izi. Ine ndikudabwa ngati alipo aliyense muno amene sanapemphereredwe, mmawa uno, ndipo inu mukudwala. Tiyezi tiwone dzanja lanu likukwezedwa mmwamba. Muyike mmwamba manja anu ngati inu mukudwala ndi osowa, ndipo inu simunapemphereredwe, mmawa uno. Palibe makadi apemphero kapena kalikonse; basi—basi odwala ndi osautsika. Chabwino.

Tiyezi tiweramitse mitu yathu kamphindi chabe.

⁸⁸ Ambuye, ndi kummero komangidwa uku, liwu la dzimbiri, oh, ine ndikupemphera kuti Inu mumize mu mtima, Mbewuyo, mulimonse, mu mtima wa anthu, kuti ife tizindikiritsidwe ndi Inu. Pakuti, ndi mwambi wakale kuno pa dziko lapansi, “Mbalame imadziwika ndi nthenga zake, ndipo munthu amadziwika ndi anthu amene akukhala nawo.” Ndipo, wokondedwa Atate Akumwamba, ife tikupemphera kuti Inu mukhale gulu lathu. Ambuye, tiloleni ife tikhale ndi Inu, ngati izo ziti zitengere chirichonse chimene ife tiri nacho pa dziko lapansi lino. Mutilole ife tizindikiritsidwe, monga, “Munthu ameneyo amakhala kwenikweni ndi Mulungu. Gulu lake ndi Mulungu.”

⁸⁹ Mulole izo zinenedwe monga izo zinali ndi Petro ndi Yohane, iwo atatha kudutsa pa chipata chotchedwa Chokongola, ndipo anati, “Ine ndiribe ndalama iliyonse; koma chimene ine ndiri nacho, ine ndikupatsani inu.” Ndipo munthu wolumalayo anachiritsidwa. Ndipo pamene pamaso pa mabwalo a milandu, anthu anati iwo anazindikira kuti iwo anali mbuli ndi osaphunzira. Iwo analibe maphunziro, koma iwo anazindikira kuti iwo anali atadzindikiritsidwa ndi gulu loyenera. Iwo amakhala ndi Yesu. Mulungu, ndicho chokhumba cha mtima wanga, kuti ndizindikiritsidwe ndi Inu, ngati mmodzi wa antchito Anu, monga mmodzi yemwe amakukondani Inu, mmodzi yemwe angamakhale woona kwa Inu, ndi kusunga zonena za Bukhu Lanu, ndi kuchita zonse zomwe ine ndikuzidziwa kuzichita, ndiko kulondola.

⁹⁰ Tsopano, Atate, kodi Inu mungatero kachiwiri usikuuno kudzizindikiritsa Nokha pakati pathu, kuti anthu akhoze kudziwa kuti ichi si chinachake basi, oh, nthawi ina yapadera, kapena—kapena chinachake mwa dongosolo limenelo, Ambuye. Mulole zidziwike usikuuno kuti Ndinu Mulungu yemweyo amene anali pano mmawa uja. Inu muli nayo Mphamvu yomweyo. Ndiponso zofanana—zinthu zomwezo zimene Inu munazichita mmawa uja, Inu mukhoza kuzichitanso usikuuno. Inu munalonjeza kuti iwo adzakhala mmasiku otsiriza.

⁹¹ Ambiri pano sakukhoza kuzindikira chikhulupiriro chokwanira. Ife tikupemphera kuti Inu muwapatse iwo chikhulupiriro tsopano. Ndipo mulole Mzimu Wanu uzindikiritsidwe pakati pathu, pakuti Inu munati, “Ntchito zimene ine ndikuzichita iyenso adzazichita, amene akukhulupirira pa Ine.” Chotero ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu muzindikiritse kuti Inu muli pano ndi ife usikuuno, ndipo muli...mumatikondabe ife. Ndipo Inu mukufuna munthu aliyense muno, yemwe sanabatizidwe, kuti abwere ndi kudzazindikiritsidwa ndi Inu. Kut iwo nawonso akakhoze kukhala ogawana nawo za chisomo chodabwitsa ichi chimene chingakhoze kusamutsidwa; kuchokera kwa ife kubwera kwa Iye, ndipo kuchokera kwa Iye kubwera kwa ife; kulakwa

kwathu kwa Iye, ndi chisomo Chake kwa ife. Perekani izi, Ambuye. Imvani mapemphero athu, pamene ife tikupempha mu Dzina la Yesu Mwana Wanu. Amen.

⁹² Ife tikuyima mu mthunzi wa chirungamo basi cha Mulungu. Nthawi iliyonse yomwe awiri kapena atatu asonkhana pamodzi mu Dzina la Yesu Khristu, Iye analonjeza kuti Iye akanadzakhala pakati pawo.

⁹³ Tsopano, ine sindikudziwa, ine ndikuganiza gawo la makadi a pemphero lachotsedwapo. Ena a inu mukhoza kukhala nawobe ena. Ambiri a inu mulibe khadi la pemphero. Ziribe kanthu kaya inu muli nalo kapena inu mulibe. Ngati mukudwala, inu mukudwala. Ndipo ngati... Mulungu Uyu Amene analemba Baibulo ili, kodi inu mukukhulupirira mwaulemu mwa Iye? Ngati Iye ati abwerere kachiwiri pakati pathu, kuti adzadzitsimikizire Yekha, kupatula kulalikira kwa Mawu, kuti Iye ali pano, kuwatsimikizira ochimwa kuti Iye ali pano; ngati Iye ali pano kuti adzachiritse odwala, ndipo adzawulula cholingacho, monga Iye anachitira pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, kodi inu mungavomereze mokondwera machiritso anu? Ngati inu mukutero, kwezani dzanja lanu, basi paliponsepo. Ife sitidzatero... ife tiribe... Ine sindingadziwe makadi apemphero omwe iye anawapatsa iwo. Ife sitikhala ndi makadi a pemphero. Basi, inu mupemphere, ndipo inu mukhulupirire.

⁹⁴ Ndipo ngati Iye ati adzachite chomwecho, ndipo adzadzizindikiritse Yekha, inu muyenera kumachita manyazi kuti musadzizindikiritse nokha ndi Iye pamenepo. Inu mukuyenera kuchita zimenezo. Tsopano, apa pali chitsutso cholunjika. Mu mpingo mmawa uno ife tinapereka makadi a pemphero, ndipo tinawaitanira iwo ku guwa, ndipo tinawapempherera iwo. Ndipo Mzimu Woyera unagwedeza ndi nthawi yopambana chomwecho, mpaka ine ndinawamverera iwo akundikokera ine kumbali, inali nthawi yoti ndizipita, chifukwa ine ndinali wofooka. Ndipo tsopano, pano ine ndikunena, inu amene mulibe makadi a pemphero, kapena chirichonse chimene inu muli, mutakhala kunja uko mwa omvetsera, inu mukutsutsa. Ine ndikukubetcherani inu kuti muchite izi, kuti mukhulupirire kuti nkhani imene ine ndakuuzani inu ya Yesu Khristu ndi Choonadi. Ndipo mupemphere, ngati mukudwala. Ziribe kanthu...

⁹⁵ Mmawa uno, ine ndinayesetsa kuti ndiwone ngati ine ndikanawapeza anthu omwe analibe kachisi. Usikuuno, ine sindikusamala kumene inu mukuchokera. Inu mungopemphera. Ndiye ngati Mzimu Woyera wawukulu uja wa Mulungu, umene ife tiri nawo chithunzi chake pamenepo, ngati Iye angabwere pakati pathu! Inu mwandimvapo ine ndikulalikira izo mochuluka kwambiri, kuti Iye anatilonjeza ife zinthu, kuti Iye akanadzachita zimenezo. Ndiyeno pamene Iye anali pa

dziko lapansi, pamene Iye anadzabwerera mu thupi lathu, Iye akanadzachita chinthu chomwecho. Tsopano, ngati mukudwala, pempherani. Ndikukubhetcherani inu!

⁹⁶ Mumubhetchere Mulungu, kuti, “Mulungu, M’bale Branham sakundidziwa ine. Iye sakudziwa kanthu za ine. Koma ngati Inu mutangomulola iye kuti atembenukire kwa ine, mudirole ine ndidzakhudze chovala Chanu, kenako Inu mudzayankhule, ine ndidzadziwa kuti Inu muli mu chilumikizo ndi mpingo uno.” Mpingo ndi okhulupirirawo. “Ndiye ine ndidzadziwa kuti Inu ndinu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Ndipo inu mupemphere.

⁹⁷ Ine ndikungomverera kutsogozedwa kuti ndichite zimenezo. Sindikudziwa chifukwa chimene ine ndinachitira, koma ine ndikumverera kutsogozedwa kuti ndichite zimenezo.

Tsopano, ngati inu mungadzutse mutu wanu.

⁹⁸ Pomwe pano, akuyang’ana pa ine, ndi mkazi wamng’ono yemwe anali ndi dzanja lake mmwamba monga *chonchi*, akupemphera, maminiti pang’ono chabe apitawo. Ndipo iye akumupempherera winawake pambali pa iyemwini. Ine sindinayambe ndamuwonapo mkaziyo mu moyo wanga, monga ine ndikudziwira. Iye ndi mlendo kwathunthu kwa ine. Koma iye akumupempherera mwana wake wamkazi, chifukwa cha opareshoni. Inu simuli ngakhale wochokera ku dziko lino. Ndinu wochokera ku Texas. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Kodi muli ndi khadi la pemphero? Inu mulibe? Inu simukusowa limodzi. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse.

⁹⁹ Ine ndikanadziwa bwanji chimene inu munali kuchipempherera? Kodi inu simukukhoza kumuwona Mulungu wa Kumwamba akuwulula zinsinsi za mu mtima? Kodi Daniele sananene zimenezo mu tsiku lake? Mulungu amaulula zinsinsi za mu mtima.

¹⁰⁰ Pali dona wakhala pafupi ndi inu pamenepo. Iye anali wokondwera kwambiri ndi zimenezo. Iye anali ndi vuto la mtima, ndipo iye akufuna kuti apemphereredwe. Chotero ngati inu mutangoyika dzanja lanu pa iye. Chabwino. Tsopano, inu mubwerere ku Chicago ndipo mukachiritsidwe. Amen. Ine sindikumudziwa mkazi ameneyo, chonchobe, sindikudziwa kanthu za iye. Koma Mulungu akukudziwani inu. Mukuona?

Iye akuzipanga Yekha kuzindikiridwa ndi ife. “Ngati inu mungakhulupirire, zinthu zonse ndi zotheka.”

¹⁰¹ Mkazi wamng’ono, wa Chiyuda uyu wakhala apayu, iye anali akupemphera, nayenso. Uko nkulondola. Inu munali kundipempherera ine kuti ndinene chinachake kwa inu. Ine ndinawona mavuto anu mmawa uno, koma ine basi sindinawatchule iwo. Koma mapazi amenewo omwe mwakhala mukuvutikana nawo, akhala bwino. Kotero musadandaule za zimenezo.

¹⁰² Inu mukukhulupirira, nanunso, dona wamng'ono mwakhala apa? Inu mukundikhulupirira ine kukhala mneneri Wake, kapena, wantchito Wake? Ine sindikukudziwani inu. Mulungu akukudziwani inu. Koma ngati Iye ali Mzimu wa Mulungu ndi ife, ndiye Iye adzachita monga Yesu anachitira. Inu munali kupemphera, ndipo zikuwoneka ngati ine ndinakopedwera kwa inu. Ndi uyo Mngelo wa Ambuye mwa iye. Ngati muti mukhulupirire, vuto lanu la mtima litha, ndi nyamakazi. Dzina lanu ndi Abiti Wisdom. Uko nkulondola. Inu mubwerere ndipo mukakhale bwino, Akazi a Wisdom. Ine sindinayambe ndamuwonapo mkaziyo mmoyo wanga.

Koma, Iye ndi Mulungu, ngati inu mutangokhulupirira izo.

¹⁰³ Apa, taonani apa. Muwone dona wamng'ono ameneyo wakhala apoyo ali ndi dzanja lake mmwamba monga *chonchi*, pa kamwa pake? Pali . . . Kodi inu simukukhoza kuwona Kuwala kuja kwapachikika pamwamba pomwe pa mkazi pamenepo? Tsopano, penyani, kukubwera kutsikira kumene kwa iye. Ine ndikukuwona Iko kukuwala. Iye ali ndi vuto ndi chiwindi, akuvutika ndi vuto la chiwindi. Ndi vuto la ndulu. Chabwino, ndinu Akazi a Palmer. Ndi zimenezotu. Ine ndikukumbukira tsopano ndi ndani. Ine sindinawone, ndi masomphenya basi; ine ndikukuwonani inu mwakhala pafupi ndi M'bale Palmer. Uko nkulondola, mlongo. Tsopano, inu mupite ndipo mukakhale bwino. Mukhulupirire, ndi mtima wanu wonse.

¹⁰⁴ Pali dona wamng'ono wakhala kumbuyo kwake, nayenso, yemwe anayang'ana mmwamba, akukhala ngati akudabwitsidwa, kumbuyo kwake komwe. Inu mukuganiza kuti vuto la msagwada la ana awiri amenewo liwasiya iwo, mlongo, ndi inu, aponso? Ndiye kazipitani pa njira yanu, kwanu, ndipo muzisangalala ndi kukhala wokondwa. Muyike dzanja lanu pa anawo, awiri onsewo ndi mavuto amenewo. Ndipo vuto lanu lachoka, nalonso. Inu mwachiritsidwa, mu Dzina la Ambuye Yesu, nonse a inu. Inu mukakhala bwino, khalani bwino.

¹⁰⁵ Kodi inu mukukhoza kumuwona Mulungu wamoyo akukhala moyo lero? Iye ndi wamkulu basi, paliponse, sichoncho Iye? Kodi inu simukufuna kuti muzindikiritsidwe ndi Iye? Ndithudi, inu mukutero. Ndithudi, inu mukufuna kutero.

¹⁰⁶ Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi chabe. Ine ndisanati . . . Izo zimandifooketsa ine mochuluka kwambiri. Ndi angati akufuna kuti akumbukiridwe mu pemphero pakali pano, akuti, "Mulungu, mundichitire ine chifundo. Ine tsopano ndikufuna kuti ndimukhulupirire Ambuye Yesu. Ine—ine ndikufuna mavuto anga onse awongoke tsopano"? Mulungu akhale ndi inu.

¹⁰⁷ Ambuye, Amene munamubweretsanso Yesu kwa akufa, Mulungu wa Kumwamba, Ine ndikukupemphani Inu, mmalo mwawo, kuti ili likhale ora limene iwo ati adzakhulupirire;

bwerani patsogolo, ngati iwo sanayambe achitapo izo kale, ndipo mudzazindikiritsidwe ndi Yesu Khristu, pano mu dziwe ili, usikuuno. Pakuti Lemba linanena, kuti, “Ngati ife tiyikidwa ndi Iye ku ubatizo, ndi kugawana naye Iye mu imfa Yake, ife tidzagawana nawo mu chiukitsiro ndi Iye.” Limenelo ndi lonjezo. Ndipo Petro Woyera wamkulu, wakale, anati kwa ife kuti, “Lapani, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo, ndipo ife tidzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.” Sabata yonse iyi. . .

¹⁰⁸ Apa pakhala mpongozi wanga wamkazi, Ambuye, Loyce wamng’ono, wanjala, ndi ludzu, ndipo akusala kudya, ndi kumadikirira. Apo pakhala mlongo wanga kumbuyo uko, wanjala, ndi ludzu, ndipo akusala kudya, ndi kumadikirira. O Ambuye, mutumize Mzimu Woyera pakali pano mwanjira ina, udzalowe mchipinda chino, ndipo ukhudze miyoyo yawo ndi Mphamvu ya chiwukitsiro. Ndipo mulole iwo adzuke pa mapazi awo, mu Mphamvu ya chiwukitsiro, ndi kudzazindikiritsidwa ndi Yesu Khristu mu chiukitsiro Chake. Perekani izi, Ambuye.

¹⁰⁹ Mukhululukire tchimo lirilonse. Muchotse chirichonse chimene chiri cholakwika, Atate, ndipo tipatseni ife chisomo Chanu, pamene ife tikupemphera mu Dzina la Yesu Khristu.

¹¹⁰ Muchiritse odwala onse ndi osautsika. Ambuye, Inu muli pano. Ndinu Mulungu. Inu, Inu mukudzitsimikizira Nokha, Mulungu. Ndipo ife tikupemphera zimenezo, podziwa chikhalidwe cha Mzimu Wanu, kuti Inu munachita zinthu pang’ono ndipo kenako munazimirira kwa iwo, munapita kwinakwake ndi kukalowa mu mzinda wina, ndipo munatuluka ndi kupita. Koma Inu munasiya chizindikiro mmbuyo, chakuti Mulungu wamoyo anakhala moyo. Ndipo ine ndikupemphera, Ambuye Yesu, kuti—kuti izi zakhala zokhutitsa pa mitima ya anthu, kuti iwo asadzaiwale konse kuti Mzimu Woyera uli pano kuti udzachiritse, ndi kudzapulumutsa, ndi kudzadzadzitsa ndi ubwino Wake. Ife tikupemphera mu Dzina la Yesu. Amen.

¹¹¹ Tsopano, ndi angati pano amene anali akuti abatizidwe? Kodi inu mungakweze dzanja lanu, amene mwakonzekera zinthu zanu. Inu mukhoza kukonzekera ndiye madzi, mu mphindi pang’ono chabe.

Ndipo tsopano pamene ife tikuyembekezera pa Mzimu Woyera, kwa mphindi pang’ono chabe. Ndi angati pano amene sanalandire Mzimu Woyera panobe, ndipo akukhumba, akupemphera modzipereka, kulandira Mzimu Woyera?

Teddy, ngati iwe ungatero, kapena ena a inu, ku limba, pomwepo. Ife tiyimba nyimbo zina pakali pano.

Pamene, akazi amene akukakonzekera ubatizo, apite ku chipinda *ichi*. Ndipo amuna apite uko ku chipinda *icho*, amene akukonzekera ubatizo. Pamene ife tikukonzekera, nafenso, kwa chochitikacho.

¹¹² Ndiyeno ife tikhala tikudikirira pa Mzimu Woyera kuti ubwere kwa ife, ndi kudzawulula kwa ife zinthu zimene Iye akufuna kuti ife tizichita.

Ndiye ife tizimitsa magetsi, muholo yayikulu. Mtumiki adzakhala ali mmadzi—cha kuno, ndipo zikatero tidza—ifetidzakhala ndi mwambo wa ubatizo.

Mphindi chabe, basi inu musanathimitse kuwalako, M'bale Evans. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge Lemba lina pamene ife tikuyembekezera, kwa mphindi chabe, ngati inu mungathe. Pamene iwo akuyamba kukonzekera, ine ndikufuna kuti ndiwerenge Lemba lina apa.

¹¹³ Ndi angati akukhulupirira kuti Mulungu ndi wopandamalire? Zedi. Iye ali pano pakali pano. Chinthu chokha chimene inu muyenera kuchita, kuti mulandire Mzimu Woyera, ndi kudzuka ndi kumulandira Iye. Bwanji, Mphamvu Yake yatsimikizira kuti Iye ali pano. Ife tingakhoze bwanji kukhala ndi mthunzi umodzi wa kukaikira? Kukhalapo Kwake kodala, koyera basi kukungosambitsa solo yathu! Ine ndikumverera ngati ine ndingafuule, pamwamba pa mawu anga, za ubwino Wake. “Ndipo chifundo Chake chimapirira kwanthawi za nthawi.” Iye ali pano. Mtima wanga ukuyaka, ndipo iwo wadzazidwa ndi chimwemwe ndi chisangalalo chopitirira, chifukwa cha Kukhalapo Kwake.

¹¹⁴ Iwo asanathimitse magetsi, ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera mu Machitidwe, mutu wa 1.

Ndipo ine ndikukhulupirira kuti munthu aliyense, mtumiki, kapena munthu muno, mlaliki, kapena zinazonse, kuti padzakhala ichi, icho, Mulungu ndi wopandamalire. Mulungu sangakhoze kuchita chinthu chimodzi mwanjira ina, ndiyeno nkudzatembenuka pamenepo ndi kudzachita *ichi*, kudzachita icho—kudzachita icho mwanjira ina. Iye ayenera kuti azichita izo mwanjira yomweyo, nthawi iliyonse. Sichoncho Iye?

Uku kunali kulengeza kumene kunapita kuchokera kwa Mulungu.

Inu amuna a Israeli, mverani mawu awa; Yesu waku Nazareti, mwamuna wotsimikiziridwa ndi Mulungu pakati panu ndi... zodabwitsa ndi zizindikiro, chimene Mulungu anachita ndi iye pakati pa inu, monga inu eniake nanunso mukudziwira:

Kodi Iye anachita zizindikiro za mtundu wanji, kuti atsimikizire kuti Iye anali Mesiya? Pakudziwa maganizo mmitima mwawo. Nkulondola uko? Zomwe Petro ananena, “Mwa zizindikiro ndi zodabwitsa, Mulungu anatsimikizira kuti Iye anali ndi Iye.”

Iye, pokhala atawomboledwa ndi uphungu wotsimikizika, kudziwiratu kwa Mulungu, inu

munamutenga, ndipo ndi manja oyipa inu munamupachika ndi kumupha Iye:

Yemwe Mulungu anamuwukitsa, atamasula zowawa za imfa: chifukwa sikunali kotheka kuti iye agwiritsitse izo.

Pakuti Davide anayankhula zokhudza iye, ine ndinawawoneratu Ambuye nthawizonse patsogolo panga, . . . iye ali pa dzanja langa lamanja, ndipo ine sindidzagwedezeke:

Chifukwa chake ndinatero ine, mtima wanga unakondwera, ndipo lirime langa linapangidwa kukondwa; kuwonjezera apo . . . thupi langa lidzapuma mu chiyembekezo:

Chifukwa inu simudzasiya solo yanga mu hade, ngakhale inu simudzamulola Mmodzi Woyera wanu kuti awone chivundi.

Inu mwadziwitsa kwa ine njira ya moyo; inu mudzandipangitsa ine kudzaza ndi chimwemwe ndi nkhope zanga.

Amuna ndi abale, ndiloleni ine ndiyankhule momasuka kwa inu za mbadwa Davide, kuti iye anafa ndipo anaikidwa mmanda, ndipo manda ake ali ndi ife mpaka lero.

Chotero pokhala mneneri, . . . podziwa kuti Mulungu analumbirira ndi lumбириro kwa iye, kuti chipatso cha mchiuno mwake, molingana ndi mnofu, iye akanadza— iye akanadzadzutsa Khristu kuti akhale pa mpando wake wachifumu;

Iye powona izi kale anayankhula za chiwukitsiro cha Khristu, kuti solo yake siinasiyidwe mu hade, ngakhale mnofu wake sunawone chivundi.

Yesu uyu Mulungu wamuukitsa, chotero ife . . . ndife mboni.

Oh, izo zinangondikondoweza ine! Ife tikadali mboni Yake. Iye anawukitsidwa kwa akufa. Iye akukhala moyo, usikuuno.

Chotero pokhala pa dzanja lamanja la Mulungu atakwezedwa, . . . atalandira za—za Atate lonjezo la Mzimu Woyera, iye wakhetsa ichi, chimene inu tsopano mukuchiwona ndi kuchimva.

Pakuti Davide sanakwere kupita . . . kumwamba: koma iye anati iyemwini, AMBUIYE anati kwa Ambuye wanga, Khala iwe pa dzanja langa lamanja,

Mpaka ine nditapanga adani ako choponderapo mapazi ako.

Chotero mulole nyumba yonse ya Israeli idziwe ndithudi, kuti Mulungu mpaka wamupanga Yesu yemweyu uyu, yemwe inu...munamupachika, zonse Ambuye ndi Khristu.

Tsopano, kodi iye amayankhula chinenero chanji, kuti zinenero zonse izo za mdziko zinamumva iye?

Tsopano pamene iwo (anthuwo) anamva ichi, iwo analaswa mu mtima mwawo, ndipo anati kwa Petro ndi...atumwi ena onsewo, Amuna ndi abale, kodi ife tichite chiyani?

Kanthawi kapitako, iwo anali “openga,” kwa iwo. Tsopano, utatha ulaliki wamphamvu uja umene unali kupita ku fuko lililonse linaima pamenepo, “Amuna ndi abale, kodi ife tingachite chiyani?” Ndiye panabwera dongosolo la kamwedwe kake. Ndiye a-...

Ndiye Petro anati kwa iwo, Lapani, ndipo mubatzidwe aliyense wa inu mu dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha tchimo, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.

Pakuti lonjezo liri kwa inu, ...kwa ana anu, ndi kwa iwo amene ali kutali, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.

Ndipo ndi kuyankhula kwina kumene iye anachitira umboni ndi kulimbikitsa, kumati, Dzipulumutse wekha kwa m’badwo wapatsogolo uno.

Ngati umenewo si Uthenga womwewo umene ife tikulalikira lero! “Dzipulumutseni nokha kwa m’badwo wapatsogolo uno.” Zizindikiro zambiri ndi zodabwitsa zikuchitidwa, Kukhalapo kwa Yesu Khristu kudzisonyeza Iyeyekha wamoyo. Ndipo ubatizo womwewo umene unatumidwa pomwe apa, ukutumidwa pomwe pano pa guwa, nawonso, usikuuno.

Ndiye iwo amene mokondwera analandira mawu ake anabatizidwa: ndipo tsiku lomwelo kunawonjezedwa kwa iwo pafupifupi miyoyo firii sauzande.

¹¹⁵ Wokonedwa Mulungu, iwo, zipindazo zayima mutadzazana anthu akuzindikiritsidwa mu ubatizo ndi Inu. Ine ndikukupemphani Inu, Ambuye, mmalo mwawo, kuti ngati Inu mwachifundo mutatero, Ambuye, pa ora lino, pamene iwo azibwera kuchokera mmadzi, mulole pakakhale chinachake chitachitika kwa iwo, kuti miyoyo yawo idzazidwe ndi Mzimu Woyera. Mulole iwo abwere ndi kuchoka mmadzi, apite patsogolo kuti akakuwonetsereni Inu mu kulalikira Uthenga, kuphunzitsa Sande sukulu, kuyankhula ndi malirime, kutanthauzira malirime, kumachita zizindikiro, zodabwitsa ndi zozizwitsa, ndipo, pamwamba pa chirichonse, chikondi cha

Mulungu chikuyaka mmiyoyo yawo, ndi kufatsa, ndi kudekha, ndi chipiriro, ndi kudzichepetsa.

¹¹⁶ Ambuye, ine ndikuwapereka iwo kwa Inu. Iwo ndi zikho za chitsitsimutso ichi. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu muwasunge iwo mu chisamaliro Chanu. Ndipo tsiku lina... Pamene ine ndaima pano kupemphera pa Baibulo Lanu, ine nditatha kulalikira kuchokera kwa Ilo, ndipo ndinalengeza ndi mtima wanga wonse chimene ine ndikuganiza kuti ndi Choonadi, monga Inu muti muwulule Izo kwa ine.

¹¹⁷ Ndipo, Ambuye, ife tikuyembekezera pa ubatizo wawo, basi pamene ife tonse tiri mwa omvetsera pano kuyembekezera chiwukitsiro. Ndipo tsiku lina, Ambuye, pamene ife tikuyima limodzi mmalo Ammwambamwamba, mulole padzabwe mkokomo wochokera Kumwamba. Lipenga lidzawomba, ndipo akufa mwa Khristu adzauka, choyamba. Mulole ife tidzakwatulidwe ndi Iye, kuti tikakomane ndi Ambuye mu mlengalenga, ndipo kwanthawizonse tikakhale ndi Iye. Perekani izi, Atate.

¹¹⁸ Tisungeni ife athanzi, ndi okondwa, ndi ozadza ndi changu. Ife sitikupempha ndalama. Ife sitikupempha zinthu zophweka. Ife tikungopempha kukhala monga Yesu. Ife tikufuna kuzindikiritsidwa ndi Iye, ndi mtundu wa Mzimu umene unali mwa Iye, wofatsa, wodekha, nthawizonse pa ntchito ya Atate.

¹¹⁹ Ambuye, mu ora lotsekera la chitsitsimutso ichi ndi kuzindikiritsidwa uku kwa ambiri a anthu ofunika, zipitirirani kudzindikiritsa Nokha, powapatsa iwo Mzimu Woyera. Perekani izi, Atate.

¹²⁰ Mudalitse kachisi wamng'ono uyu, mumudalitse mtumiki aliyense, munthu aliyense amene wabwerako, mpingo uliwonse umene wakhala uli kuno.

¹²¹ Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu mutumize chitsitsimutso mu mpingo uliwonse kudutsa mdziko lonseli. Ndipo ife tidzawawona iwo akubwera pamodzi ndi mtima umodzi ndi mgwirizano umodzi, kwa chisomo chokwatulitsa cha Yesu Khristu kuti chiperekedwe pakati pathu. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu. Amen.

¹²² Tsopano magetsi azizima, mu holo yayikulu, kwa kanthawi. Mipango iyi yapemphereredwa. Ndipo tsopano magetsi azimitsidwa kwa kanthawi kakafupi chabe, ndiyeno—ndiyeno mungokhala chete. Ndipo mtumikiyo akhala akubatiza, mmodzi mmodzi pambuyo pa mzake, mpaka ife titawatsiriza iwo.

[Abale akonzanso zipangizo za pa nsanja pokonzekera utumiki wa ubatizo—Mkonzi]. Tsopano ngati aliyense akhoza kuwona...

¹²³ Tsopano, ndipo maikrofoni imodzi imeneyo, ikokereni pansi maikrofoni imeneyo pa thanki pamenepo. Eya. Uko

nkulondola. [Winawake asunthe chiyimitsira maikrofoni—Mkonzi]. Zikuwoneka bwinoko. Eya. [M'bale akuti, “Izo ziri chomwecho kuti ife tizijambulira izo mwabwino kwenikweni.”] Ichi ndi cha kwa wojambula? [“Inde.”] Chabwino. Iye akusamalira zimenezo.

¹²⁴ Ine ndimafuna kuti ndichite izi, inemwini, usikuuno. Ine ndatenthedwa kwambiri zedi. Ndipo M'bale Neville wakhala akupumula, kotero ife tikufuna m'busa kuti akhale ndi chinachake chochita ndi izi, nayenso, m'bale wabwino kwambiri.

¹²⁵ Mphindi chabe, magetsi azimitsidwa, mu holo yayikulu, zikatero inu muzitha kumawona, pogwiritsa ntchito galasi lalikulu lapachikika kumbuyo kwake, limayang'ana pansi kumene mu dziwe kumene iwo akhale akubwera, kuti adzabatize, mwamsanga pamene iwo akuwakonzekeretsera iwo.

¹²⁶ Ndipo nthawi iliyonse, pamene iwo akubatiza, amakhala... ma eledara amakokera katani. Zimenezo zimatetezera...kwa akazi, pamene iwo akulowa ndi kutuluka mmadzimo. Ndipo kotero ndiye iwo adzakhala akubwera, mmodzi pambuyo pa mzake. Inu mudzitchula dzina lanu, kunena yemwe inu muli, ndi kuwabatiza iwo mu Dzina la Yesu Khristu.

¹²⁷ Tsopano, kumbukirani, monga—monga mtumiki chabe, woyankhira pa Uthenga uwu umene waperekedwa kwa ine, ine ndingalimbikitse izo kwa aliyense amene sanabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, inu mubatizidwenso. Ndicho chimene Paulo ananena. Ngakhale pamenepo, pamene iwo anali atabatizidwa mwanjira ina, popanda Dzina, iye anati iwo ayenera kuti abatizidwenso, mu Dzina la Yesu Khristu.

¹²⁸ Iye anati, “Ngati Mngelo abwera, nadzaphunzitsa china chirichonse, msiyeni iye akhale wotembereredwa.” Zimenezo zikupezeka mu Agalatiya. Agalatiya, mutu wa 1, ndi ndime ya 8. “Ngakhale ife, kapena Mngelo wochokera Kumwamba, akalalikira uthenga wina uliwonse, iye akhale kwa inu wotembereredwa.”

[Chotchinga chobatizira chatsegulidwa—Mkonzi].

¹²⁹ Tsopano, basi mwambo usanayambe, kodi aliyense akukhoza kuwona? [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]... anatsikira mmadzi a imfa. Ife tsopano tikuwajowina atumiki a Uthenga, potero ife...?...[Malo opanda kanthu pa tepi.] Mzanga weniweni wa ine, wochokera kumusi uko...?...Dona uyu ndi bwenzi wapamtima kwambiri kwa Oral Roberts; iye ndi mwamuna wake...?...msilikari wina wamkulu, wopindulira moyo kwa Mulungu wopambana, M'bale Oral Roberts, mmodzi wa abwenzu anga apamtima, nayenso. [Malo opanda kanthu pa tepi.] Inde. 

59-1220E Kuzindikiritsidwa ndi Khristu
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2025 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org